BOMA LA MALAWI

PULOGALAMU YOLIMBIKITSA KUCHILIMIKA KU NGOZI ZOGWA MWADZIDZIDZI NDI KUSINTHA KWA NYENGO (RCRP-2)

# BUKU LA NDONDOMEKO YOLANDILIRA NDI KUTHETSERA MADANDAULO

Unduna Wa Zachuma Ndi Mapulani Achitukuko
Nthambi Yokonza Mapulani A Chitukuko Ndi Chuma
P.O. Box 30136
Lilongwe 3
Phone: +265 (0) 1 788 888
Fax: +265 (0) 1 788 247/131

JULY, 2025

# ZAMKATIMU


Mau Otsogolera i
Mau Wothokoza ii
Ndandanda Wa Mawu Achidule iii

**1.0. CHIYAMBI 1**

1.1. Za Pulogalamu ya RCRP-2 1
1.2. Njira Yolandilira ndi Kuthetsera Madandaulo 3

**2.0. KASANJIDWE KA NDONDOMEKO YOLANDILIRA NDI KUTHETSERA MADANDAULO MU PULOGALAMU YA RCRP-2 13**

2.1. Ndondomeko zolandilira ndi kuthetsera madandaulo 13
2.2. Mfundo zomwe makomiti a m'dera (GCRMCs) adzitsata pothana ndi madandaulo 13
2.3. Mfundo zomwe komiti yoyangánira za msamuko idzitsata 15
2.4. Mfundo zomwe komiti yothana ndi madandaulo a ogwira ntchito (WGRMC) idzitsata 16
2.5. Mfundo zomwe komiti yomvetsera ndi kuthana ndi madandaulo ya m'dera (AGRMC) idzitsata 18
2.6. Mfundo zomwe makomiti othana ndi madandaulo a pa boma ndi mmizinda idzitsata 20
2.7 Ntchito za komiti yothetsa madandaulo ya dziko lonse (NGRMC) 22

**3.0. NJIRA ZOLANDILIRA NDI KUTHETSERA MADANDAULO 25**

3.1. Gawo 1: Kulandira Madandaulo 25
3.2. Gawo 2: Kuunika, Kusanthula ndi Kuyankha 26
3.3. Gawo 3: Kuthetsa ndi Kutseka Madandaulo 27
3.4. Gawo 4: Buku Lolembamo Madandaulo (GRM Registry) 27
3.5. Gawo 5: Kuunika ndi Kuyang'anira GRM 27

**4.0. NJIRA ZINA ZOTUMIZA MADANDAULO NDI MAYANKHO 29**

4.1. Kutumiza Madandaulo Mwachindunji ku RCRP-2 PCU 29
4.2. Kupeza Thandizo ku GRM ya World Bank 30

**5.0. NKHANI ZAPADERA 31**

5.1. Milandu yaupandu 31
5.2. Kugwiritsa ana ntchito zoposa misinkhu yawo 31
5.3. Kuzembetsa ana 31
5.4. Nkhanza Zochitika Chifukwa cha Kusiyana Pakati pa 31 Amayi ndi Abambo komanso zokhudza kugonana 31
5.5. Mchitidwe wa Tsankho ndi Katangale Polemba Kapena Kusankha Anthu Opindula ndi Pulogalamu ya RCRP-2

**MNDANDANDA WA ZOONJEZERA 39**



# CHIYAMBI

Mu zaka makumi angapo zapitazi, dziko la Malawi lakhala likukhudzidwa ndi ngozi za kusefukira kwa madzi zoposa phambu zisanu ndi zinayi. Zotsatira za posachedwapa, zikuonetsa kuti phamvu komaso chiwerengero cha ngozichi chakhala chikukwera kwambiri mmadera a mmatawuni ndi mmizinda. Pofuna kuchepetsa zotsatira za ngozi zomwe zimachitika chifukwa cha kusintha kwa nyengo, Boma la Malawi lakhazikitsa Pulogalamu Yolimbikitsa Kuchilimika ku Ngozi Zogwa Mwadzidzidzi ndi Kusintha kwa Nyengo (RCRP-2) yomwe cholinga chake ndi kuonetsetsa kuti mayiko ndi okonzeka kuthana ndi ngozi zogwa mwadzidzidzi zomwe zimachitika pafupipafupi ndipo zimakhudza kwambiri miyoyo ya anthu, zomangamanga ndi zachilengedwe.

Pofuna kukwaniritsa zochitika zonse za pulogalamuyi, RCRP-2 yakhazikitsa Buku la Ndondomeko Yolandilira ndi Kuthetsera Madandaulo (GRM). Bukuli likupereka ndondomeko zotsogolera kupewa, kuperekera ndi kuyankha madandaulo onse okhudza pulogalamuyi. Ndondomekozi zikulunjika pothandiza komanso kuthana ndi madandaulo okhudza ufulu wa anthu, makamaka kwa omwe akukhudzidwa kapena kupindula nawo ndi ntchito za pulogalamuyi.

Malamulo Aakulu Oyendetsera Dziko Lino (Constitution) amalimbikitsa kuteteza ndi kulemekeza ufulu wachibadidwe wa nzika zonse. Mwachindunji, Gawo 13 la Malamulo a Dziko lino limalimbikitsa kusasiyana pakati pa amuna ndi akazi, kusintha umoyo wa anthu akumudzi, kuteteza zachilengedwe, ufulu wa ana komanso kuthetsa mikangano mwamtendere.

Choncho, Malamulo a Dziko la Malawi amalimbikitsa nthambi za boma kukonza ndondomeko ndi nsanamira zolimbikitsira ntchito zolemekeza ndi kuteteza maufulu achibadidwe, chisamaliro ndi chitukuko cha anthu. Mogwirizana ndi izi, Boma la Malawi lidakhazikitsa malamulo ndi ndondomeko zosiyanasiyana zolimbikitsira maufulu kuphatikizapo: Malamulo Osamalira za Chilengedwe a m'chaka cha 2017; Malamulo Oona kuti Palibe Kusiyana Pakati pa Amayi ndi Abambo a m'chaka cha 2013; Malamulo Oona Chisamaliro , Chitetezo ndi Chilungamo cha Ana a m'chaka cha 2010; Malamulo Oona za Chipepeso ndi Kapezedwe ka Malo a m'chaka cha 1997 ; Malamulo a Kalembedwe ka Ntchito a m'chaka cha 2000; ndi Malamulo Oona za Ntchito a m'chaka cha 2000. Malamulo ndi ndondomeko zemenezi ndi zina mwa zomwe zinaunikidwa pokonza bukuli. .

Kuwonjezera apo, buku la Masomphenya a Dziko lino la Malawi 2063, ndime yachiwiri ikutsindika za ulamuliro wabwino ndi ndondomeko zakagwiridwe kabwino ka ntchito za boma, makamaka kulimbikitsa kuti pakhale ulamuliro wabwino komanso chilungamo. Izi zingatheke pokhapokha ngati nzika zikupatsidwa mwayi kuti zidzipereka maganizo ndi kugwiritsa ntchito ufulu wawo wachibadidwe , pokwaniritsa zofuna zawo komanso kuthetsa mikangano yawo. Choncho, kulephera kuthana ndi madandaulo otumphuka chifukwa cha kukhazikitsidwa kwa pulogalamu ya RCRP-2 kungathe kupereka chiopsezo cholepheletseratu zolinga zolimbikitsa ulamuliro wabwino .

Ndondomeko Yolandilira ndi Kuthetsera Madandaulo yabwino ndi yofunikira kwambiri kuti pulogalamuyi iziyenda bwino. Ndili ndi chikhulupiliro kuti kugwiritsa ntchito bukuli kuthandiza kukwaniritsa zolinga za pulogalamuyi.

Choncho, ndikupempha onse okhudzidwa kuti adzipereke pokhazikitsa komanso kulimbikitsa ntchito za Ndondomeko Yolandilira ndi Kuthetsera Madandaulo okhudza RCRP 2.

Patrick Zimpita

**MLEMBI WAMKULU**

**NTHAMBI YOKONZA MAPULANI A CHITUKUKO NDI CHUMA**



# MAU OTSOGOLERA

Boma la Malawi, kudzera mu Unduna wa Zachuma ndi Chitukuko (MoFEA), likuyendetsa pulogalamu ya zaka zisanu (2024-2028) yothandizira kuchilimika ku ngozi zogwa mwadzidzidzi ndi kusintha kwa nyengo (RCRP-2) kum'mwera ndi kum'mawa kwa Africa. Cholinga chachikulu cha pulogamuyi ndi kuchepetsa mavuto amene amabwera chifukwa cha kusintha kwa nyengo.

Pali kuthekera kwakuti kayendetsedwe ka Pulogalamu ya RCRP-2 kangadzetse madandaulo osiyanasiyana. A ena mwa madandaulowa ndi monga: nkhanza zochitirana chifukwa cha kusiyana pakati pa amuna ndi akazi, mchitidwe wogwilirira, mchitidwe wokakamiza zogonana, zachinyengo, kupereka malipiro ochepa kapena kuchedwetsa malipiro, kukaniza malo kuti pagwiridwe ntchito, kulowelera malo a eni , kuba ndi zina zotero. Kuonjezera apo, madandaulo ena omwe angatumphuke ndi monga kusakhutitsidwa ndi kaperekedwe ka katundu komanso kulandidwa malo.

Ndondomeko yolandilira ndi kuthetsera madandauloyi idzithandiza pulogalamuyi kuwunikira madandaulo komanso kupeza njira zothana nawo mwachangu ndi mwachilungamo. Izi zidzithandiza kuti mikangano isakule n'kukhala mavuto aakulu.

Njirayi ndi yosavuta, yachangu, yosalira ndalama zambiri komanso yolimbikitsa mbali zokhudzidwa kukhutira ndi zotsatira. Ndondomeko yolandilira ndi kuthetsera madandaulo ikuyenera kukhala yofikirika, yothandiza anthu mwachangu, yopereka danga kwa onse pothana ndi mikangano komanso kusagwirizana. Njirayi ndi chiyambi chomvera madandaulo koma siikulowa mmalo mwa njira zina zothetsera madandaulo monga malamulo a boma kapena mabwalo a milandu (makhothi).

Kakonzedwe ka bukuli kanatsatira njira zomva maganizo a anthu osiyanasiyana. Mwa zina, kakonzedwe ka bukuli kanasanthula ndondomeko zina zomwe zilipo kale kuphatikizapo kuwunika mabuku a pulogalamu ya RCRP-2, ndondomeko zolimbikitsa kuteteza ndi kusamala zachilengedwe, zokambirana ndi akadaulo ochokera ku mabungwe komanso unduna ndi nthambi za boma zosiyanasiyana.

Pomaliza, ndiyamikire anthu ogwira ntchito ku RCRP -2 ku ma office onse atatu (PCU, PIU-RA ndi PIU-NLGFC) chifukwa cha upangiri wapadera womwe anapereka pokonza bukuli.

Adwell Zembele

**PROGRAMME COORDINATOR**

# MAU WOTHOKOZA

Buku ili latheka chifukwa cha kugwirana manja ndi ukadaulo wa anthu onse omwe akugwira ntchito za RCRP -2. Koma mwapaderadera, ndithokoze anthu awa chifukwa cha kudzipereka ndi kutaya nthawi yawo pokonza buku ili;

| NAME | POSITION | INSTITUTION |
|---|---|---|
| Aubrey Chaguzika | Social Safeguards Specialist | Regional Climate Resilience Programme (RCRP 2)-PCU |
| Chimwemwe Chisenga Tembo | Social Safeguards Specialist | Regional Climate Resilience Programme (RCRP 2)-PCU |
| Emmanuel Mkomwa | Environmental Safeguards Specialist | Regional Climate Resilience Programme (RCRP 2)-PCU |
| Victor Nyirongo | Environmental Safeguards Specialist | Regional Climate Resilience Programme (RCRP 2)-PCU |
| Yvonne Sundu | Communication Specialist | Regional Climate Resilience Programme (RCRP 2)-PCU |
| Boston Kadzamira | Social Planning Officer | Roads Authority |
| Felistas Kamzati Ndilowe | Social Safeguards Specialist | Regional Climate Resilience Programme (RCRP 2)-PIU-RA |
| Joanna Medellina Mbeye | Senior Environmental Planning Officer | Roads Authority |
| Chawanangwa Soko | Social Safeguards Specialist | National Local Government Finance Committee (NLGFC) |
| Helbert Bolokonya | Environmental Safeguards Specialist | National Local Government Finance Committee (NLGFC) |
| Chipiliro Khamula | PRO | Department of Disaster Management Affairs (DoDMA) |
| Joseph Chimbuto, PhD | Communication Specialist | Malawi Education Reform Programme |
| Alick Kampeza | Principal Unity Officer and PRO | Ministry of Local Government, Unity and Culture |
| Biswick Mlaviwa | Chief Environmental Officer | Environmental Affairs Department |
| Victoria Kamanga | Principal Local Government Services Officer | Ministry of Local Government Unity and Culture |
| Ronald Phiri | Deputy Director | Ministry of Gender, community Development and Social Welfare |

# NDANDANDA WA MAWU ACHIDULE

| | |
|---|---|
| ADC | Area development Committee |
| AGRMC | Area Grievance Redress Mechanism Committee |
| AIDS | Acquired Immune - Deficiency Syndrome |
| CAG | Community Action Group |
| CAT | Convention against Torture |
| CEDAW | Convention for the Elimination of Discrimination against Women |
| CERC | Contingent Emergency Response Component |
| CGRMC | Community Grievance Redress Mechanism Committee |
| CRC | Convention on Rights of the Child |
| CSO | Civil Society Organizations |
| CVSU | Community Victim Support Unit |
| DCCMS | Department of Climate Change and Meteorological Services |
| DEC | District Executive Committee |
| DGO | District Gender Officer |
| DGRMC | District Grievance Redress Management Committee |
| DODMA | Department of Disaster Risk and Management Affairs |
| DPD | Director of Planning and Development |
| DRMO | Disaster Risk Management Officer |
| DSWO | District Social Welfare Officer |
| DWR | Department of Water Resources |
| E&S | Environmental and Social |
| EAD | Environmental Affairs Department |
| ESS | Environmental and Social Safeguards |
| GBV | Gender Based Violence |
| GRM | Grievance Redress Mechanism |
| GRMC | Grievance Redress Mechanism Committee |

| | |
|---|---|
| **HIV** | Human Immuno-deficiency Virus |
| **ILO** | International Labor Organization |
| **MEPA** | Malawi Environment Protection Authority |
| **MoF** | Ministry of Finance |
| **MOFEA** | Ministry of Finance and Economic Affairs |
| **MoGCDSW** | Ministry of Gender, community Development and Social Welfare |
| **MoL** | Ministry of Labour |
| **MoTPW** | Ministry of Transport and Public Works |
| **NGO** | Non – Governmental Organizations |
| **NGRMC** | National Grievance Redress Mechanism Committee |
| **NLGFC** | National Local Government Finance Committee |
| **PAPs** | Project affected persons |
| **PCU** | Project Coordinating Committee |
| **PIU** | Project Implementation Unit |
| **PSC** | Project Steering Committee |
| **PTC** | Project Technical Committee |
| **RA** | Roads Authority |
| **RCRP-2** | Regional Climate Resilience Programme |
| **SEA** | Sexual Exploitation and Abuse |
| **SH** | Sexual Harassment |
| **SRH** | Sexual and Reproductive Health |
| **STIs** | Sexually Transmitted Diseases |
| **UEC** | Urban Executive Committee |
| **VAC** | Violence against Children |
| **VAWG** | Violence Against Women and Girls |
| **VDC** | Village Development Committee |
| **WFP** | World Food Programme |
| **WGRMC** | Workers Grievance Redress Mechanism Committee |

# 1 CHIYAMBI



Figure 1: Mkumano wofunsa maganizo a anthu okhudzidwa ndi pulojekiti pa bukhu la madandaulo-Nchalo Chikwawa

## 1.1 KUFOTOKOZA ZA PULOGALAMU

Boma la Malawi, kudzera mu Unduna wa Zachuma ndi Chitukuko (MoFEA), likuyendetsa pulogalamu ya zaka zisanu (2024-2028) yothandizira kuchilimika ku ngozi zogwa mwadzidzidzi ndi kusintha kwa nyengo (RCRP-2) Kum'mwera ndi Kum'mawa kwa Africa. Ili ndi gawo lachiwiri la pulogalamuyi. RCRP-2 ikuthandizidwa ndi Banki yaikulu pa dziko lonse (World Bank) ndi ndalama zokwana US$250 miliyoni. Mwandalamazi, US$240 miliyoni ndiyothandizira dziko la Malawi pomwe US$10 miliyoni ndiyothandizira African Union (AU). Ntchito za pulogalamuyi zikuchitika m'maboma onse 28 a m'dziko lino, ndipo zina mwa ntchitozi zikuchitika ku chigwa cha mtsinje wa Shire komanso mmadera a m'chigawo chapakati ndi kum'mwera kwa Malawi. Pulogalamuyi ikuyendetsedwa komanso kuyang'aniridwa ndi Project Coordination Unit (PCU) yomwe ili mkati mwa Nthambi ya Chitukuko ndi Chuma (EP &D) pansi pa Unduna wa Zachuma ndi Mapulani a Chitukuko. Ena mwa omwe akuthandizira ntchitoyi pansi pa PCU ndi (Nthambi Yooona za Ngozi Zogwa Mwadzidzidzi (DoDMA), Nthambi Yoona Zanyengo ndi Kusintha Kwanyengo (DCCMS), Nthambi Yoona za Nkhalango (Forestry), Bungwe Loona za Kagwiritsidwe ndi Kasamalidwe ka Madzi (NWRA), Nthambi Yoona Zosamalira Nthaka (Land Resources), Nthambi Yoona za Chisamaliro cha Madzi (DWRS), Makhonsolo a mmizinda ya Blantyre ndi Zomba pamodzi ndi ma ofesi awiri oyendetsa ntchito za pulogalamuyi (PIUs); yomwe imodzi ili ku Bungwe Loona za Misewu (RA) pansi pa Unduna wa Zamtengatenga ndi Ntchito Zomangamanga (MoTPW), ndipo inayo ili ku Bungwe Loona za Kayendetsedwa ka Ndalama M'maboma Ang'onoang'ono (NLGFC) pansi

pa Unduna wa Maboma Aang'ono, Umodzi ndi Chikhalidwe (MoLGUC). Cholinga chachikulu cha pulogamuyi ndi kulimbikitsa kuchilimika ku zovuta zobwera chifukwa chakusintha kwa nyengo monga kusefukira kwa madzi ndi chilala.

Ntchito za RCRP-2 ziri ndi magawo asanu (5) omwe akuthandiza kukwaniritsa cholinga cha pulogalamuyi. Magawowa ali motere:

### GAWO LOYAMBA (1): KAPEZEDWE KA NDALAMA NDI NTCHITO ZOLIMBIKITSA KUCHEPETSA CHIOPSEZO CHA KUSINTHA KWA NYENGO

Cholinga cha gawo ili ndi kulimbikitsa luso ndi ukadaulo pa kasamalidwe ndi katetezedwe ka chilengedwe monga kukolora madzi ndi kudzala mitengo. Gawoli lidzathandiziranso kapezedwe ka ndalama ndi ntchito zolimbikitsa kuchepetsa chiopsezo cha kusintha kwa nyengo.

### GAWO LACHIWIRI (2): KULIMBIKITSA NDI KUSAMALIRA NTCHITO YA ZOMANGAMANGA POLIMBANA NDI KUSINTHA KWA NYENGO

Gawo ili likulimbikitsa ntchito yomanganso zinthu zomwe zidaonongeka ndi Namondwe wa Freddy. Gawo ili lithandizanso makhonsolo kuchilimika ku mavuto obwera chifukwa cha kusintha kwa nyengo. Kudzera mu Bungwe la African Union, gawoli lilimbikitsanso ntchito zakafukufuku wa kusefukira kwa madzi komanso ng'amba.

### GAWO LACHITATU (3): NTCHITO ZOTHANDIZIRA MADERA KUKHALA OCHILIMIKA KU MAVUTO A KUSINTHA KWA NYENGO

Gawo ili likulimbikitsa anthu am'matauni kukonzekera komanso kutenga nawo gawo pokonza ndondomeko zochepetsera chiopsezo cha m'madera awo. Izi zithandiza kuti anthuwo atenge nawo gawo pokonza ndondomeko zothandizira okhudzidwa ndi mavuto obwera chifukwa cha kusintha kwa nyengo. Gawoli lithandizanso kukonza ndondomeko zopezera opindula ndi thandizo pakati pa anthu okhudzidwa mmizinda ya Blantyre ndi Zomba. Gawoli likhazikitsanso ntchito za mthandizi moyeselera m'matauni ndi cholinga cholimbikitsa kuchilimika ku mavuto obwera chifukwa cha kusintha kwa nyengo.

### GAWO LACHINAYI (4): KAYENDETSEDWE KA PULOGALAMU (RCRP-2)

Gawo ili likuthandizira kupereka ndalama za kayendetsedwe ka RCRP-2 monga kugula zipangizo ndi zinthu zina zofunikira komanso kupereka ukadaulo pofuna kuonetsetsa kuti pulogalamuyi ikutsatira ndondomeko zomwe Banki yaikulu pa dziko lonse (World Bank) imatsatira pa kasamalidwe ka ndalama, miyoyo ya anthu ndi Chilengedwe. Gawo ili likuthandiziranso ntchito zosiyanasiyana monga: kayendetsedwe, kalondolondo komanso kaperekedwe ka malipoti a mmene pulogalamuyi ikuyendera.

### GAWO LACHISANU (5): THUMBA LOTHANDIZIRA PA NGOZI ZADZIDZIDZI

Gawo ili lidzigwira ntchito kukagwa ngozi yadzidzidzi. Izi zimatengera boma kulengeza kuti m'dziko mwagwa ngozi yadzidzidzi ndipo pakufunika thandizo la msanga. Mwachitsanzo, pa 23 March mchaka cha 2025, Boma la Malawi lidalengeza kuti maboma 23 mwa maboma 28 ndi malo angozi chifukwa cha ng'amba yomwe idadza ndi nyengo ya El Niño. Nyengoyi idadzetsa mvula yochepa ndi kusefukira kwa madzi zomwe zidaononga mbeu komanso kuchepetsa zokolola. Zonsezi zidachitika chifukwa cha kusintha kwa nyengo. Potsatira izi, bungwe la World Food Programme (WFP) lidayamba ntchito yogula chakudya cha ndalama zokwana US$5 miliyoni.

Pamene ntchito za RCRP-2 zikugwiridwa, anthu kapena magulu atha kukhudzidwa mosiyanasiyana. Madandaulo omwe angaperekedwe atha kukhala okhudza umoyo wa anthu komanso zachilengedwe. Pachifukwachi, pakuyenera kukhala ndondomeko za mmene okhudzidwa angathandizidwire pa madandaulo awo mwachangu, mowona mtima, momveka bwino, komanso mosagwiritsa ntchito ndalama zambiri. Choncho, RCRP-2 yakhazikitsa ndondomeko kapena njira yolandilira ndi

kuthetsera madandaulo

## 1.2. NJIRA YOLANDILIRA NDI KUTHETSERA MADANDAULO

### 1.2.1. Tanthauzo

Njira Yolandilira ndi Kuthetsera Madandaulo imatanthauza dongosolo ndi ndondomeko zomwe zimakhazikitsidwa mwapadera ndi pulogalamu ndi cholinga cholandira ndi kuthana ndi mikangano, nkhawa komanso kupereka mayankho pa mavuto amene angakhalepo pakagwiridwe ka ntchito. Zolandiridwa mu ndondomekoyi zimalembedwa ngati madandaulo, mapempho, mayankho kapena liwu lililonse lofanana ndi mawu ngati amenewa mmatanthauzo. Njirayi imathandiziranso kudziwa ngati pulogalamu ikuyenda mwadongosolo chifukwa imapereka tsatanetsatane wa momwe ntchito ikuyendera.

Ndondomeko yolandilira ndi kuthetsera madandaulo ikuyenera kukhala yofikirika, yothandiza anthu mwachangu, yopereka danga kwa onse pothana ndi mikangano komanso kusagwirizana. Njirayi ndi chiyambi chomvera madandaulo koma siikulowa mmalo mwa njira zina zothetsera madandaulo monga malamulo a boma kapena makhothi.

### 1.2.2. Kufunika Kwa Ndondomeko Yolandilira ndi Kuthetsera Madandaulo Pansi pa RCRP-2

Pali kuthekera koti Pulogalamu ya RCRP-2 ingadzetse madandaulo osiyanasiyana. Ena mwa madandaulowa ndi monga: nkhanza zochitirana chifukwa cha kusiyana pakati pa amayi ndi abambo , mchitidwe wogwilirira, mchitidwe wokakamiza zogonana, zachinyengo, kupereka malipiro ochepa kapena kuchedwetsa malipiro, kukaniza malo kuti pagwiridwe ntchito, kulowelera malo a eni , kuba ndi zina zotero. Kuonjezera apo, madandaulo ena omwe angatumphuke ndi monga kusakhutitsidwa ndi kaperekedwe ka katundu komanso kulandidwa malo.

Ndondomeko yolandilira ndi kuthetsera madandauloyi idzithandiza pulogalamuyi kuwunikira madandaulo komanso kupeza njira zothana nawo mwachangu ndi mwachilungamo. Izi zidzithandiza kuti mikangano isakule n'kukhala mavuto aakulu. Njirayi ndi yosavuta, yachangu, yosalira ndalama zambiri komanso yolimbikitsa mbali zokhudzidwa kukhutira ndi zotsatira.

Kukambirana ndi kugwirizana pakati pa makomiti omva madandaulo, magulu oyendetsa ntchito za pulogalamuyi ndi anthu okhudzidwa kudzipereka mpata woyambilira wothetsera madandaulo. Ngakhale izi ziri motere, ogwira ntchito ku Pologalamu ya RCRP-2 adzipereka upangiri komanso kuthandizira kukhazikitsa ndi kulimbikitsa makomiti Olandira ndi Kuthetsa Madandaulo (GRM) omwe alipo kale m'madera osiyanasiyana.Levels to assist in the redress process.

### 1.2.3. Zolinga za Ndondomeko Yolandilira ndi Kuthetsera Madandaulo

Zolinga zazikulu za ndondomekoyi ndi monga izi:

1. Kukhazikitsa chikhulupiliro ndi kukambirana pakati pa onse okhudzidwa ndi Pologalamu ya RCRP-2.
2. Kulimbikitsa umwini ndi kukhazika kwa ntchito zonse zogwiridwa mu pulogalamuyi.
3. Kuteteza ma ufulu a anthu oponderezedwa ndi omwe alibe mau.
4. Kupeza madandaulo omwe angadze mkatikati mogwira ntchito za pulogalamuyi.
5. Kuonetsetsa kuti mikangano yokhudza ntchito za pulogalamuyi ikukambidwa mwapadera komanso mopatsidwa nthawi yokwanira.
6. Kuonetsetsa kuti nthawi yogwira ntchito za RCRP-2 sizikusokonekera chifukwa chofuna kuthana ndi madandaulo.
7. Kuthandiza kuchepetsa nthawi komanso ndalama zimene okhudzidwa angawononge posakasaka chilungamo ku mabwalo ena.

### 1.2.4. Njira Zomwe Zagwiritsidwa Ntchito

## Pokonza Buku Lolandilira ndi Kuthetsera Madandaulo

Kakonzedwe ka bukuli kanatsatira njira zomva maganizo a anthu osiyanasiyana. Mwa zina, kakonzedwe ka bukuli kanasanthula ndondomeko zina zomwe zilipo kale kuphatikizapo kuwunika mabuku a pulogalamu ya RCRP-2, ndondomeko zolimbikitsa kuteteza ndi kusamala chilengedwe, zokambirana ndi akadaulo ochokera ku mabungwe komanso unduna ndi nthambi za boma zosiyanasiyana.

Tebulo liri m'munsiri likufotokoza mwachidule m'ndandanda wa omwe anatenga nawo mbali pokonza bukuli.

**TEBULO LOYAMBA: OMWE ANATENGA NAWO MBALI PA KAKONZEDWE KA BUKULI**

| SN | KOGWILIRA NTCHITO | OMWE ADATENGAPO GAWO POKONZA BUKULI |
|---|---|---|
| 1 | **Maunduna ndi Nthambi za boma** | • Maunduna ndi nthambi zomwe zikuyendetsa nawo ntchito za mu pulogamuyi: Unduna wa za Nkhalango, Unduna wa Zamalimidwe, DoDMA, DCCMS,, RA, MoFEA, EAD, DWSS, DWRS, NLGFC<br>• Maunduna ndi nthambi zokhudzidwa: MoLGUC, MoGCDSW, MEPA.<br>• Mamembala a Programme Steering Committee.<br>• Mamembala a Programme Technical Committee. |
| 2 | **Makhonsolo a pa boma ndi mmizinda** | Mkulu wokonza mapulani achitukuko (DPD), Ofisala woona za ngozi zogwa mwadzidzidzi (DRMO), Ofisala woona za chisamaliro cha anthu (DSWO), Ofisala wolimbikitsa ntchito zoti pasakhale kusiyana pakati pa amayi ndi abambo (DGO) Ofisala woyang'anira zolemba anthu ntchito (DLO) , Ofisala woona za malo (DLO), Apolisi, a mabwalo a milandu, ndi mabungwe omwe si aboma. |
| 3 | **Anthu oimira madera osiyanasiyana** | Atsogoleri a m'madera, alangizi , ma CBO, achitetezo cha m'mudzi,, mamembala a komiti yoona za ngozi zogwa mwadzidzidzi, magulu a amayi, azipembedzo ndi ena ambiri. |

### 1.2.5. Ogwiritsa Ntchito Buku Lolandilira ndi Kuthetsera Madandaulo mu Pulogalamu ya RCRP-2

Ena mwa ogwiritsa ntchito bukuli ndi awa:

#### Maunduna ndi Nthambi za Boma

Maunduna ndi nthambi za boma kuphatikizapo oyendetsa pulogalamuyi monga: Unduna wa Zachuma ndi Mapulani a Chitukuko (MoFEA), Unduna Owona kuti Pasakhale Kusiyana Pakati pa Amayi ndi Abambo Chitukuko cha Mmadera ndi Chisamaliro cha Anthu (MoGCDSW), Unduna wa Maboma Aang'ono, Umodzi ndi Chikhalidwe (MoLGUC), Unduna wa za Mtengatenga ndi Ntchito Zomangamanga, (MoTPW), Unduna Woona Zantchito (MoL), Bungwe Loyang'anira Ndalama Zoyendetsera Maboma Aang'ono (NLGFC), Bungwe Loyang'anira za Misewu (RA), Nthambi Yoona za Ngozi Zogwa Mwadzidzidzi (DoDMA), Nthambi Yoona Zachilengedwe (EAD), Nthambi Yoona za Nyengo ndi Kusintha kwa Nyengo (DCCMS), , Nthambi Yoona za Madzi (DWR), Nthambi Yoyang'anira Chitukuko cha Madzi (DWS), Bungwe Loona za Kagwiritsidwe ndi Kasamalidwe ka Madzi (NWRA) Unduna wa Zamalimidwe, Nthambi Yoona za Nkhalango, Bungwe Loteteza Zachilengewe (MEPA), Nthambi ya Mabwalo a Zamilandu, Apolisi, Ogulitsa katundu ndi zinthu zina, Programme Coordinating Unit ndi Programme Implementation Units.

#### Makhonsolo a pa Boma ndi Mmizinda

Mamembala onse a makomiti olandilira ndi kuthetsera madandaulo pa khonsolo ndi mmadera (DGRM/CGRM), alangizi, makomiti akuluakulu a mmakhosolo a pa boma ndi mmizinda (UEC, DEC) a malonda ndi ogulitsa katundu osiyanasiyana komanso mabungwe omwe si aboma.

#### Anthu Oimira Madera Oiyanasiyana

Magulu onse a m'madera okhudzidwa ndi pulogalamu ya RCPR-2 monga atsogoleri, a ADC, a VDC, amisiri, anthu a m'mudzi, alangizi ndi a luso la zomangamanga.

### 1.2.6. Mfundo Zoyendetsera Ndondomeko Zolandilira ndi Kuthetsera Madandaulo mu Pologalamu ya RCRP-2

Mfundo zotsatirazi ndi zomwe zitsogolere ndondomeko yolandilira ndi kuthetsera madandaulo:

**Umunthu:** Mfundoyi ikulimbikitsa kufunikira kolemekeza maufulu a chibadwidwe omwe aliyense ali nawo.

**Kusasalana:** Mfundoyi ikutsindika ganizo loti munthu wina aliyense sakuyenera kusalidwa pa zifukwa monga izi: Kukhala wammuna kapena wamkazi, zaka, thanzi la moyo wake, kukhala wa pa banja kapena ayi, chipembedzo, chipani chake cha ndale kapena mtundu.

**Chilungamo:** Mfundo iyi ikuzindikira kuti pali kusiyana pakati pa anthu komwe kukuyenera kulimbikitsidwa popanga zinthu zofanana ndi kapezedwe ka zinthu zotukula miyoyo yawo. Magulu omwe akuyenera kulimbitsidwa ndi monga amayi, achinyamata komanso oponderezedwa.

**Kusasiyana pakati pa abambo ndi amayi:** Mfundoyi ikulimbikitsa pulogalamuyi kuwonetsetsa kuti amayi, abambo ndi achinyamata ali ndi mwayi wofanana wotenga nawo gawo ndi kupeza zinthu zofunikira ndi zopindulira miyoyo yawo. Izi zikutanthuza kuika ndondomeko zotukulira kuthekera kwa amayi ndi achinyamata pokwaniritsa zolinga zawo mu pulogalamu ya RCRP-2.

**Kuchita Zinthu Mwandondomeko:** Mfundoyi ikulimbikitsa adindo ndi aliyense kupanga ziganizo ndi kugwira ntchito mogwirizana ndi malamulo.

**Kufikirika:** Mfundoyi ikuonetsetsa kuti Ndondomeko Yolandilira ndi Kuthetsera Madandaulo ipezeke mosavuta kwa aliyense ndipo isakhale ndi zotsamwitsa monga: chiyankhulo, kusadziwa kulemba ndi kuwerenga, kusowekera chidziwitso, kusowekera kwa ndalama , kapena kukhala ndi mantha pa zotsatira za madandaulo. Ndondomekoyi yakonzedwa kuti idzikhala

yosavuta kufikirika kwa onse okhudzidwa kuti adzithandizidwa mwachangu.

**Zodziwikiratu:** Mfundoyi ikuwonetsetsa kuti ndondomekoyi ipereke dongosolo lomveka bwino pa kalandiridwe ndi kathetsedwe ka madandaulo. Ndondomekoyi ikulimbikitsanso kuti pakhale tsatanetsatane wa nthawi ya kagwiridwe ka ntchito ndi zotsatira zake.

**Chilungamo:** Mfundoyi ikulimbikitsa ndondomeko zosakondera makamaka pa kapezedwe ka mauthenga ndi mwayi wothandizira kutenga nawo mbali popanga ziganizo.

**Kugwirizana ndi malamulo ndi maufulu:** Mfundoyi ikutsindika kuti zotsatira za zolandilira ndi kuthetsera madandaulo ndi zogwirizana ndi malamulo aakulu oyendetsera dziko lino komanso maufulu osiyanasiyana. Ndondomekoyi siikuletsa okhudzidwa kutsata njira zina zopezera chilungamo monga kukamang'ala ku mabwalo a milandu kapena ku polisi.

**Kuchita zinthu poyera:** Mfundoyi ikutsindika kufunika koti zotsatira za madandaulo zikhale poyera, komanso zopezeka mu ziyankhulo ndi njira zosiyanasiyana kwa aliyense.

**Kuthekera pa zinthu:** Mfundoyi ikulimbikitsa pulogalamu ya RCRP-2 kukhazitsa njira zokwezera ukadaulo ndi maluso oyenera ndi cholinga chokwaniritsa ntchito yolandilira ndi kuthetsera madandaulo.

**Mayankho:** Mfundoyi ikuvomereza kufunika koti onse okhudzidwa ndi pulogalamu ya RCRP-2 adzipereka tsatanetsatane wa mayankho (feedback) kapena maganizo awo pa momwe pulogalamuyi ikuyendera. Izi zidzithandiza pulogalamuyi kuyenda bwino komanso kupindulira Amalawi.

### 1.2.7. Kayendetsedwe Koyenera ka Ndondomeko Yolandilira ndi Kuthetsera Madandaulo

Kayendetsedwe ka ndondomeko Yolandilira ndi Kuthetsera Madandaulo a RCRP -2 kakuyenera kumvetsedwa bwino ndi onse ogwiritsa ntchito ndondomekoyi. Pakuyenera kukhala kulumikizana kwabwino pakati pa onse ogwiritsa ntchito ndondomekozi. Ntchito za ndondomekozi zikuyenera kulandira thandizo lokwanira.

Kuti izi zikwaniritsidwe, ndondomekoyi ikuyenera kutsatira mfundo izi:

**a. Kudziwitsa Anthu za Ndondomeko Yolandilira ndi Kuthetsera Madandaulo mu Pulogalamu ya RCRP-2**

Njira Yolandilira ndi Kuthetsera Madandaulo ikuyenera kukhala mbali imodzi yofalitsira mauthenga a mu pulogalamu ya RCRP-2. Mauthenga ofalitsa komanso kuphunzitsa anthu za ndondomekoyi adziulutsidwa kudzera pa wayilesi yomvera ndi ya kanema, misonkhano yosinasiyana komanso kugawa timabuku ta mauthenga. Pofuna kuti idzipezeka mosavuta, ndondomekoyi yatanthauziridwa mu Chichewa. Mauthengawa adzipezekanso pa tsamba la intaneti (www.rcrp.gov.mw).

**b. Kapezedwe ka Thandizo Logwirira Ntchito ya Ndondomeko Yolandilira ndi Kuthetsera Madandaulo mu Pulogalamu ya RCRP-2**

Pulogalamu ya RCRP-2 ndi yodzipereka kuti ndondomeko Yolandilira ndi Kuthetsera Madandaulo ikwaniritse zolinga zake. Pulogalamuyi idzionetsetsa kuti ikupereka zipangizo ndi ndalama zokwanira monga kupereka mabuku ndi mafomu olembamo madandaulo omwe adzipezeka mmaboma, mmizinda ndi mmadera osiyanasiyana. Makomiti oyendetsa ntchito Yolandira ndi Kuthetsa Madandaulo apatsidwa mphavu zopereka mabuku ndi mafomu omwe mwalembedwamo madandaulo kwa oyendetsa ntchito za pologalamu.

**c. Kulimbikitsa Luso**

Makomiti oyendetsa ntchito Yolandira ndi Kuthetsa Madandaulo aphunzitsidwa zoyenera kutsatira kuti agwire ntchito yawo moyenera ndi mwachangu komanso moonetsetsa kuti anthu okhudzidwa ndi okhutira ndi

kagwiridwe ka ntchito yawo.

**d. Kalondolondo wa Ntchito Yolandilira ndi Kuthetsera Madandaulo**

Pulogalamu ya RCRP-2 yakhazikitsa njira zochitira kalondolondo ndi kuthandizira kutsatira za mmene ndondomekoyi ikugwilira ntchito. Nthawi zina ogwira ntchito yoyendetsa ntchito ya Pulogalamuyi adzakhala ndi udindo owunika za mmene ndondomekoyi ikugwilira ntchito. Kuti izi zitheke, mwa zina, njira ziwiri izi zidzitsatidwa: Njira yoyamba; makomiti adzipereka mabuku ndi mafomu omwe alembedwa kale madandaulo kwa oyendetsa ntchito yoyendetsa pulogalamuyi. Njira yachiwiri ndi kupereka mwayi kwa okhudzidwa kupereka madandaulo awo mwachindunji kwa omwe akuyendetsa ntchito za pulogalamuyi pamene akuona kuti sakuthandizidwa mwa changu. Madandaulo okhudza nkhanza za pakati pa mamuna kapena mkazi komanso kugonana adziperekedwa ku bungwe lapadera lomwe lidziyangánira nkhani zoterezi.

**e. Kulumikizitsa ndondomeko Yolandilira ndi Kuthetsera Madandaulo**

Akatswiri owona zachitetezo cha anthu kudzera mwa ogwira ntchito ku pulogalamuyi adzionetsetsa kuti ndondomeko yolandilira ndi kuthetsera madandaulo ikuyenda molumikizika bwino. Akatswiri owona zachitetezo cha anthu awiri ochokera ku mabungwe omwe akutumikira pulogalamuyi (RA ndi NLGFC) adzakhala ndi udindo oyendetsa makomiti Olandira ndi Kuthetsa Madandaulo m'magawo onse a pulogalamu ya RCRP -2.

## 11.2.8. Madandaulo Omwe Angaperekedwe Mu Ndondomeko Yolandilira ndi Kuthetsera Madandaulo

Kuyendetsa pulogalamu ya RCRP-2 kungadzetse madandaulo osiyanasiyana monga awa:

- Kulandidwa kwa malo kapena katundu, kapena kuletsedwa kugwiritsa ntchito malo.
- Nkhanza zomwe zingadze chifukwa cha ntchito yogwirika mu pulogalamuyi.
- Kutsekedwa kwa njira zomwe anthu amadutsa.
- Chinyengo ndi mchitidwe wa katangale.
- Kuphwanyidwa kwa ufulu wachibadwidwe.
- Nkhanza zochitirana pakati pa amayi ndi abambo.
- Nkhanza zokhudza ntchito.
- Ntchito zogwiridwa mosalongosoka. Kuchedwa kumaliza ntchito.
- Kugwiritsa ana ntchito zopyola msinkhu wawo.
- Kuwonongeka kwa mpweya, madzi, nthaka ndi phokoso.
- Kulowetsa ndale pa ntchito.
- Mapulani a zomangamanga osalongosoka.
- Kuba ndi milandu ina yaupandu.
- Ngozi za pantchito.

**TEBULO LACHIWIRI: KUTAMBASULA MADANDAULO OMWE ANGAPEREKEDWE**

<table>
<tr><th>SN</th><th>MTUNDU WA DANDAULO</th><th>ZITSANZO</th><th>KUTAMBASULA KWAKE</th></tr>
<tr><td>1</td><td>Kulandidwa kwa malo ndi katundu.</td><td>Mikangano ya malo ndi katundu wa anthu m’dera.</td><td>• Pali kuthekera kuti ntchito zomangamanga zomwe ziri mu zigawo 1, 2 ndi 3 zitha kulowerera malo a eni komanso kudzetsa mikangano.<br>• Kupereka chiletso choti anthu asafike malo ena omwe kukugwiridwa ntchito.<br>• Kuchedwa kupereka chipepeso cha ndalama kwa omwe anapereka malo awo kuti pagwiridwe ntchito.</td></tr>
<tr><td>2</td><td>Nkhanza zochitirana pakati pa amayi ndi abambo.</td><td>Nkhanza zogonana, kugwilirira, nkhanza kwa amayi ndi atsikana, kumenya mkazi kapena mamuna.</td><td>• Kuwumirizidwa kugonana ndi antchito a zomangamanga kapena makontarakita kuti apeze mwayi wa ntchito kapena ganyu.<br>• Ogwira ntchito ya zomangamanga kugonana ndi anthu a m’dera posinthana ndi zinthu zina monga ndalama.<br>• Kuchita ubwenzi ogonana ndi ana, kugwilirira komanso kugwira malo obisika.<br>• Ndemanga zonyazitsa amayi ndi atsikana a m’dera.<br>• Kumenyedwa ndi mamuna kapena mkazi chifukwa chotenga nawo gawo pa ntchito ya RCRP-2.<br>• Kuponderezedwa pa ntchito za mu pulogalamu chifukwa choti ndiwe mayi.<br>• Nkhanza zilizonse zimene zingadze posalana chifukwa choti wina ndi wamkazi kapena wammuna mkatikati moyendetsa ntchito za mu pulogalamu ya RCRP-2.</td></tr>
<tr><td rowspan="4">3</td><td rowspan="4">Nkhanza za pa malo a ntchito</td><td>Kagawidwe ka ntchito.</td><td>• Kagawidwe ka ntchito kokondera potengera kuti ndi mamuna kapena mkazi. Mwachitsanzo, amayi kugwira ntchito zosafuna luso lapadera.</td></tr>
<tr><td>Kugwiritsa ntchito anthu mokakamiza.</td><td>• Kuwakakamiza anthu kugwira ntchito mwa kusafuna kwao chifukwa cha chinyengo kapena kuwopseza.</td></tr>
<tr><td>Kuphwanya malamulo antchito.</td><td>• Kuchedwetsa malipiro kapena kulipira malipiro ochepera mlingo okhazikitsidwa ndi boma.<br>• Kugwira ntchito nthawi yaitali komanso yotaika monga usiku kwambiri.<br>• Kupatsidwa ntchito kwa nthawi yochepa monga mwezi umodzi basi.</td></tr>
<tr><td>Umoyo ndi chitetezo pa malo ogwilira ntchito.</td><td>• Kuvulala pa ntchito.<br>• Kusowekera kwa zida zodzitetezera (PPE).<br>• Kusowekera kwa zipinda zothandizira ukhondo monga zimbudzi.<br>• Kusapatsidwa chipepeso atachita ngozi pa malo a ntchito.<br>• Ngozi zazikulu.<br>• Imfa yodza chifukwa cha ngozi yochitika pa malo a ntchito.</td></tr>
</table>

| SN | MTUNDU WA DANDAULO | ZITSANZO | KUTAMBASULA KWAKE |
|---|---|---|---|
| 4 | Nkhanza zokhudza ana | Nkhanza kwa ana. | • Kugwiriridwa kwa ana komanso kuwakakamiza kukwatiwa.<br>• Kuphwanya ufulu wa ana, mwa zina monga kumanga zinthu zina pa malo ochitira masewera.<br>• Kusiya kusamalira ana chifukwa chotanganidwa ndi ntchito za mu pulogalamu ya RCRP-2. |
| | | Kugwiritsa ana ntchito zopyola msinkhu wao. | • Kugwiritsa ntchito ana achichepere mmalo mwa makolo awo komanso kulemba ntchito ana achichepere.<br>• Kugwiritsa ntchito ana achichepere pa chitukuko cha m'dera. |
| 5 | Chinyengo ndi katangale | Kugula katundu mosatsata ndondomeko komanso kuba. | • Kuumiriza a malonda kuti apereke ziphuphu.<br>• Mchitidwe wa kuba zipangizo pa malo a ntchito zomangamanga. Kukakamiza opindula ndi pulogalamu ya RCRP-2 kugawana ndi omwe sakuyenera kupindula nawo.<br>• Kukhala ndi mndandanda wa maina abodza a anthu oti apindule pa thandizo la mu pulogalamuyi asali enieni. |
| 6 | Kuphwanya ufulu wa anthu wachibadwidwe | Kuchitira nkhanza anthu chifukwa chotengapo gawo pa ntchito za Pulogalamu ya RCRP-2. | • Nkhanza zimene oyendetsa pulogalamu ya RCRP-2 kapena owatumikira atha kuchitira anthu a m'dera.<br>• Kugwiritsa ntchito mawu onyazitsa.<br>• Kumenya opindula kapena ogwira ntchito za pulogalamu ya RCRP-2. |
| 7 | Zokhudza chilengedwe | Kuonongeka kwa mpweya, madzi, phokoso, komanso kugwedezeka kwa nthaka. | • Kutulutsa fumbi, kutaya zoipa mwachisawawa, phokoso lochokera ku makina ogwirira ntchito zomangamanga komanso kuuma kwa mitsinje chifukwa cha kudzadza kwa mchenga.<br>• Kuwonongeka kwa madzi chifukwa chogwiritsa ntchito mankhwala.<br>• Madandaulo okhudza kusowekera kwa ukhondo kwa ogwira ntchito zomangamangazo.<br>• Kupha nyama zakutchire mosavomerezeka, kuotcha makala, kudula mitengo mwachisawawa.<br>• Kuonongeka kwa zomera ndi nyama za chilengedwe chifukwa cha ntchito ya zomangamanga.<br>• Kubweretsa zomera zoopsa ku chilengedwe cha malowo.<br>• Nyama ndi zomera zomwe ziri pachiwopsezo choti zitha osadzapezekanso.<br>• Kutaya zoipa mopanda dongosolo.<br>• Kukumba mchenga omangira mosatsata malamulo.<br>• Kutayika kwa zinthu zamadzimadzi zowononga chilengedwe. |

| SN | MTUNDU WA DANDAULO | ZITSANZO | KUTAMBASULA KWAKE |
|---|---|---|---|
| 8 | **Umoyo ndi chitetezo cha anthu a m'dera** | **Ngozi, kuvulala, kapena zovuta zomwe zingadze chifukwa cha ntchito za pulogalamu ya RCRP-2** | • Ngozi, kuvulala, kapena zovuta zina kwa ogwira ntchito m'dera chifukwa chosapatsidwa zodzitetezera (PPE) kapena maphunziro achitetezo.<br>• Ngozi zokudza chifukwa chosatsata ndondomeko zoteteza umoyo monga malire a liwiro la galimoto lovomerezeka kapena kuyika mipanda yoteteza malo omwe pakumangidwa.<br>• Matenda opatsirana pogonana mosadziteteza monga HIV ndi AIDS, mimba zosakonzekera chifukwa cha zibwenzi zogonana.<br>• Kubuka kwa miliri ya matenda monga cholera, malungo, COVID-19 ndi ena. |
| 9 | **Kulowetsa ndale mu pulogalamu ya RCRP-2** | | • Atsogoleri andale atha kugwiritsa ntchito za chitutuko cha zomangamanga ngati chida chokopera anthu kuti adzawavotere, komanso kupomboneza kaganizidwe ka anthu. |
| 10 | **Mapulani akamangidwe** | | • Mapulani ena amasonkhezera ngozi monga milatho yosamangidwa bwino yomwe siimakhala ndi njira zokwanira zodutsira madzi. Izi zimachititsa madzi kusefukira. |

**TEBULO LACHITATU: MALAMULO, NDONDOMEKO KOMANSO MAPANGANO OMWE AMATSOGOLERA KAYENDETSEDWE KA MILANDU MOLEMEKEZA UFULU WACHIBADWIDWE**

| SN | ZINTHU | KUMASULIRA |
|---|---|---|
| 1 | **Mapangano amene maiko anagwirizana mmene angatetezere ufulu wa anthu awo.** | • Pangano la maiko lotsindika za maufulu achibadwidwe a munthu lokhazikitsidwa m'chaka cha 1948.<br>• Pangano la maiko lotsindika ufulu wa anthu komanso pa ndale lokhazikitsidwa m'chaka cha 1966.<br>• Pangano loletsa kuzunza, nkhanza, komanso mchitidwe onyazitsa kapena zilango lomwe linakhazikitsidwa m'chaka cha 1984 (CAT).<br>• Pangano loletsa tsankho lirilonse kwa amayi (CEDAW).<br>• Pangano la Ufulu wa Ana (CRC).<br>• Pangano la ufulu wa anthu komanso ufulu wa amayi ku Africa (lomwe lidasayinidwa ku Maputo, m'dziko la Mozambique).<br>• Pangano la maiko lokhudza kusintha kwa nyengo (Climate Change) lokhazikitsidwa m'chaka cha 1992.<br>• Pangano la maiko loona zamoyo zosiyanasiyana lokhazikitsidwa m'chaka cha 1992.<br>• Pangano loletsa kutaya nyasi kapena zoopsa m'maiko a eni lomwe lidakhazikitsidwa ku Basel m'dziko la Switzerland.<br>• Pangano la maiko loletsa kugwiritsa ntchito ana zoopsa lomwe lidakhazikitsidwa mchaka cha 1999.<br>• Pangano la maiko loletsa kukakamiza anthu kugwira ntchito.<br>• Pangano la maiko lolimbikitsa kulipira malipiro mosakondera.<br>• Pangano la maiko loletsa mchitidwe wosalana kapena wa tsankho. |
| 2 | **Malamulo a Dziko Lino** | • Malamulo aakulu a Dziko la Malawi (makamaka maufulu komanso gawo 24, mwa zina).<br>• Lamulo loletsa nkhanza m'banja lomwe lidakhazikitsidwa m'chaka cha 2006 (lidaunikidwanso mu 2022).<br>• Lamulo loona kuti pasakhale kusiyana pakati pa amayi ndi abambo lokhazikitsidwa m'chaka cha 2013 (lidaunikidwanso mu 2022).<br>• Lamulo loona chisamaliro cha ana, chitetezo komanso chilungamo lokhazikitsidwa m'chaka cha 2010.<br>• Lamulo loletsa kuzembetsa anthu lomwe lidakhazikitsidwa m'chaka cha 2015.<br>• Lamulo la maukwati, kutha kwa banja ndi maubale lomwe lidakhazikitsidwa m'chaka cha 2015.<br>• Lamulo loona kasamalidwe ka chilengedwe lomwe lidakhazikitsidwa m'chaka cha 2017.<br>• Lamulo la malo lokhazikitsidwa m'chaka cha 2016 lomwe lidaunikidwanso m'chaka cha 2022.<br>• Lamulo la kapezedwe ka malo komanso lamulo lokhudza chipepeso lokhazikitsidwa m'chaka cha 2022.<br>• Lamulo loona malo amakolo lomwe lidakhazikitsidwa m'chaka cha 2022.<br>• Lamulo loona chitetezo, umoyo pa ntchito komanso chisamaliro lomwe lidakhazikitsidwa m'chaka cha 2014.<br>• Lamulo loona mapulani a malo lomwe lidakhazikitsidwa m'chaka cha 2016.<br>• Lamulo la ntchito lomwe lidakhazikitsidwa m'chaka cha 2010 ndipo lidaunikidwanso m'chaka cha 2021.<br>• Lamulo loona za chipepeso cha ovulala pa ntchito lomwe lidakhazikitsidwa m'chaka cha 2000.<br>• Lamulo loona maubale a pantchito lomwe lidakhazikitsidwa m'chaka cha 2000. |

| SN | ZINTHU | KUMASULIRA |
|---|---|---|
| 3 | **Ndondomeko za Dziko** | • Ndondomeko yoona kuti palibe kusiyana pakati pa amai ndi abambo lokhazikitsidwa m'chaka cha 2015 (makamaka gawo 7).<br>• Ndondomeko ya dziko ya kachepsetsedwe ka chiopsezo cha ngozi zogwa mwadzidzidzi yomwe idakhazikitsidwa m'chaka cha 2015.<br>• Ndondomeko yoona za malo yomwe idakhazikitsidwa m'chaka cha 2002.<br>• Ndondomeko yothana ndi mliri wa HIV ndi AIDS yomwe idakhazikitsidwa m'chaka cha 2016.<br>• Ndondomeko ya kasamalidwe ka zinthu zopezeka pa nthaka yokhazikitsidwa m'chaka cha 2000.<br>• Ndondomeko ya katayidwe ka nyasi (E-waste) yokhazikitsidwa m'chaka cha 2024.<br>• Ndondomeko yothana ndi kusintha kwa nyengo yokhazikitsidwa m'chaka cha 2016. |
| 4 | **Mapulani akuluakulu a dziko** | • Mapulani othana ndi nkhanza za pakati pa amayi ndi abambo (National Action Plan to Combat Gender-Based Violence) omwe adagwira ntchito pakati pa 2016 ndi 2021.<br>• Mapulani a zakasamalidwe ka zamoyo zosiyanasiyana omwe adagwira ntchito kuyambira chaka cha 2015 mpaka 2026.<br>• Mapulani a kasamalidwe ka zonyasa. |

# 2 KASANJIDWE KA NDONDOMEKO YOLANDILIRA NDI KUTHETSERA MADANDAULO MU PULOGALAMU YA RCRP-2

## 2.1 NDONDOMEKO ZOLANDILIRA NDI KUTHETSERA MADANDAULO

Makomiti olandira ndi kuthetsa madandaulo pansi pa Pulogalamu ya RCRP-2 adzikhazikitsidwa pa magawo anayi motere:

a. **Makomiti am'dera kapena mu wodi (CGRMCs/ Ward GRMCs):** Adzikhazikitsidwa m'madera kapena malo omwe ntchito zomangamanga zikuchitika. Ngati komiti ya CGRMC/WGRMC ilipo kale, RCRP-2 idziwalimbikitsa komanso kuwaonjezera mphamvu pofuna kuonetsetsa kuti ali ndi kuthekera kokwanira kothana ndi madandaulo odza chifukwa cha pulogalamuyi.

b. **Komiti yoyangánira za msamuko:** Makomitiwa adzikhazikitsidwa ku madera komwe kuli ntchito za zomangamanga zomwe zingakhudze kusamutsa anthu kapena katundu.

c. **Komiti ya ogwira ntchito pamalowo (WGRMC):** Idzikhazikitsidwa pamalo omwe ntchito ya zomangamanga ikuchitikira.

d. **Komiti yothana ndi madandaulo a m'dera ya Mfumu Yaikulu (AGRMC):** Idzigwira m'dera la mfumu yaikulu komwe pulogalamuyi ikuchitikira. Ngati komiti ya AGRMC ilipo kale, pulogalamu ya RCRP-2 idziwadzutsa kapena kuyionjezera mphamvu pofuna kuonetsetsa kuti ili ndi kuthekera kokwanira kothana ndi madandaulo okudza ndi pulogalamuyi.

e. **Komiti yothana ndi madandaulo pa boma kapena mu mzinda (DGRMCs/City GRMCs):** Idzikhazikitsidwa pa khonsolo ya boma kapena mzinda. Ngati khonsolo ili kale ndi makomiti ogwira ntchito ngati zimenezi pansi pa mapulojekiti ena, RCRP-2 idziwaonjezera mphamvu ndi ukadaulo wina othandizira kuthana ndi madandaulo okhudza pulogalamuyi.

f. **Komiti yothana ndi madandaulo ya ku likulu la Boma (NGRMC):** Ikhazikitsidwa ku likulu la Boma komwe adziyendetsa ndondomeko yothetsa madandaulo okhudza madera onse omwe RCRP-2 ikugwira ntchito zake.

## 2.2. MFUNDO ZOMWE MAKOMITI A M'DERA (GCRMCS) ADZITSATA POTHANA NDI MADANDAULO

Komitiyi ikhazikitsidwa m'madera omwe ntchito za Pulogalamu ya RCRP-2 zikugwirika. Komitiyi ikhazitsikidwa m'midzi (village) kapena m'dera la Gulupu (Group Village) kutengera ndi ntchito zomwe zikugwiridwa. Mafumu kapena andale sadzaloledwa kukhala mamembala a komitiyi. Mafumu a m'madera adzakhala olangiza komanso owunikira zinthu zina chabe koma osati kukhala mamembala a komitiyi. Komitiyi ikuyenera kumadziwitsa mafumu za madandaulo omwe yalandira kuti mafumuwo athandizepo mu njira zina. Komitiyi ikuyenera kuthana ndi madandaulo mkati mwa sabata ziwiri.

### 2.2.1. Oyenera kukhala membala mu komiti ya ku dera (CGRMC)

Komitiyi idzikhala ndi mamembala eni-eni a m'dera, kuphatikizirapo ogwira ntchito za boma amene ali adindo oyendetsa pulogalamuyi. Munthu

mmodzi wa m'dera ndi amene asankhidwe kukhala wapampando ndipo mlembi wa komitiyo akhala wogwira ntchito zaboma. Mamembala a komitiyi ayenera kukhala okhulupirika komanso a mbiri zabwino. Amayi osachepera anayi (4) pa anthu khumi (10) alionse ayenera kukhala mamembala a komitiyi. Akatswiri ena adzisankhidwa ngati pakufunika kutero. Komiti ya m'dera ya AGRMC idzithandizira zisankho za wapampando ndi mlembi omwe adzitumikira m'maudindo awo kwa zaka zonse za pulogalamuyi.

Mamembala a komitiyi ndi awa:

1. Munthu m'modzi oyimira anthu a m'dera omwe apindule ndi pulogalamuyi.
2. Ogwira ntchito m'boma m'deralo (okhudzidwa ndi pulogalamu) – Mlembi.
3. Oyimira azipembedzo.
4. Oyimira komiti ya m'dera kapena wodi yoona za ngozi zogwa mwadzidzidzi.
5. Oyimira anthu aulumali.
6. Oyimira achinyamata (ochokera ku gulu kapena bungwe la achinyamata m'deralo).
7. Oyimira amayi (ochokera ku gulu kapena bungwe la amayi m'deralo).
8. Oyimira komiti yachitukuko m'mudzi – Wapampando.
9. Oyimira mabungwe omwe si aboma (kuphatikizirapo ma CBO).
10. Oyimira gulu la achitetezo cha m'dera.
11. Oyimira komiti ya m'dera yomwe ikukhudzidwa ndi pulogalamu.
12. Oyimira komiti yoona za malo kapena alembi a malo.

### 2.2.2. Ntchito ndi maudindo a komiti ya m'dera (CGRMC)

Komitiyi idzikhala yoyamba kulandira madandaulo okhudza Pulogalamu ya RCRP-2 ndipo idzigwira ntchito izi:

- Kuchititsa misonkhano yodziwitsa anthu za ndondomeko zolandilira ndi kuthana ndi madandaulo mogwirizana ndi makomiti a m'dera/m'boma/mmizinda.
- Kulandira ndi kulembera madandaulo onse ochokera kwa amene akukhudzidwa ndi pulogalamuyi.
- Kuwunika madandaulo onse amene alandiridwa.
- Kufufuza ndi kupeza njira yothetsera madandaulo.
- Kumva ndi kulandula madandaulo.
- Kusunga mndandanda wa momwe madandaulo aliri komanso mmene ena athetsedwera.
- Kutumiza ku makomiti a m'dera/m'boma/mmizinda madandaulo amene sanatheke kuti akachitepo kanthu.
- Kutumiza milandu yokhudza nkhanza pakati pa amayi ndi abambo (monga zomenyana, kugwilirira, ndi zina zotero) ndi milandu ina yaupandu koyenelera monga ku Polisi kuti akachitepo kanthu.
- Kudziwitsa odandaula za mmene madandaulo awo akuthandizikira.
- Kupereka malipoti pa mwezi uliwonse kwa makomiti a pa boma/mzinda komanso kudziwitsa mafumu za momwe zinthu zikuyendera.

### 2.2.3. Kasanjidwe ka misonkhano

Komiti idzikumana mwezi uliwonse mkatikati mwa Pulogalamu ya RCRP-2 komwe ntchito za zomangamanga zikuchitikira kapena m'madera omwe akukhudzidwa ndi ntchitozo.

Komitiyi ikhoza kusintha kuchuluka kwa misonkhano yake malingaw ndi momwe madandaulo akufikira. Madandaulo ena ndiofunika kuthana nawo mwachangu popanda kudikira nthawi ya misonkhano yokhazikika. Madandaulo awa akukhudza nkhani za nkhanza pakati pa amayi ndi abambo monga zogonana komanso milandu yaupandu.

### 2.2.4. Ndondomeko za misonkhano

- Wapampando wa komiti ndi yemwe adzitsogolera. Ngati wapampando palibe, munthu wina ogwirizira wapampando adzitsogolera msokhanowu.
- Mlembi wa komiti ndi yemwe adziitanitsa misonkhano, kulembera zokambirana za misonkhanoyi, kugawa zomwe zalembedwa komanso kuonetsetsa kuti zasainiridwa ndi kusungidwa.
- Chiwerengero choyenera chovomerezeka kutimsonkhanowakomitiuchitike(quorum) chiyenera kukhala mamembala osachepera theka (50 pelesenti) la mamembala oyenera kupezeka. Mwachitsanzo, ngati komiti ili ndi anthu khumi (10) ndipo pamsonkhanopo pabwera anthu asanu (5) msokhano ukuyenera kuchitika chifukwa anthuwo ndi theka la ma membala a komiti.
- Komiti idzitsatira mfundo zolimbikitsa kuchita zinthu poyera komanso mwachilungamo nthawi zonse.
- Kutengera ndi dandaulo kapena mlandu, odandaula omwe akukhudzidwa ndi pulogalamuyiadzipemphedwakukaonekera ku bwalo lomva dandaulo lawo. Ngakhale ziri chonchi, odandaulayo sakuloledwa kukhalapo pa milandu ina monga ya umbanda. Madandaulo okhudza amuna ndi akazi komanso kugonana, adzitumizidwa ku bungwe lapadera lothandizira kugwira ntchito zimenezi pansi pa RCRP-2.

### 2.2.5. Malo ochitira misonkhano

Komiti idzichititsa misonkhano yake pa malo omwe ali pafupi ndi mamembala ake kapena pa malo amene kukugwirika ntchito ya pulogalamuyi.

### 2.2.6. Kufalitsa zotsatira zomwe komiti yagwirizana pa dandaulo

Komitiyi izidziwitsa odandaulo zotsatira za chigamulo chake mkati mwa masiku asanu ndi awiri (7) kuchokera tsiku lomwe adagwirizana za chigamulo.

### 2.2.7. Katumizidwe ka malipoti

Komiti idzipereka malipoti ku makomiti a m'dera/paboma/m'mizinda. Komiti idzigwira ntchito limodzi ndi makomiti a m'dera/paboma/m'mizinda pa nkhani zonse zomwe zatumphuka komanso mmene madandaulo akuyendera. Komitiyi idzikhala ikulumikizana ndi makomiti ena oyendetsa nawo pulogalamuyi ngati pakufunika kutero.

## 2.3. MFUNDO ZOMWE KOMITI YOYANGÁNIRA ZA MSAMUKO IDZITSATA

Komitiyi ikhazikitsidwa m'madera omwe ntchito za Pulogalamu ya RCRP-2 zikugwirika makamaka komwe kungafunikire msamuko.

### 2.3.1. Oyenera kukhala membala mu komiti ya ku dera (CGRMC)

Komitiyi ikhala ndi mamembala eni eni a m'dera, kuphatikizirapo ogwira ntchito za boma amene ali adindo oyendetsa pulogalamuyi. Munthu mmodzi wa m'dera ndi amene asankhidwe kukhala wapampando wa komitiyi. Ndipo Mlembi wa komitiyo akhala wogwira ntchito za boma. Mamembala a komitiyi ayenera kukhala okhulupilirika komanso a mbiri zabwino. Amayi osachepera 40 pa anthu 100 alionse ayenera kukhala mamembala a komitiyi. Akatswiri ena asankhidwa ngati pakufunika kutero. Komiti ya m'dera ya CGRMC idzithandizira zisankho za wapampando ndi mlembi omwe adzatumikire kufikira nkhani za msamuko zitatha.

Mamembala a komitiyi ndi awa:

1. Munthu m'modzi oyimira anthu a m'dera amene akukhudzidwa ndi za msamuko.
2. Ogwira ntchito m'boma m'deralo (okhudzidwa ndi Pulogalamu) – Mlembi
3. Oyimira a zipembedzo.
4. Oyimira anthu aulumali.
5. Oyimira achinyamata (ochokera ku gulu kapena bungwe la achinyamata m'deralo).

6. Oyimira amayi (ochokera ku gulu kapena bungwe la amayi m'deralo).
7. Oyimira komiti yachitukuko m'mudzi.
8. Oyimira mabungwe omwe si aboma (kuphatikizirapo ma-CBO).
9. Oyimira gulu la achitetezo cha m'dera.
10. Oyimira komiti yoona za malo kapena alembi a malo.

### 2.3.2. Ntchito ndi maudindo a komiti ya m'dera (CGRMC)

Komitiyi idzikhala yoyamba kulandira madandaulo okhudza Pulogalamu ya RCRP-2 ndipo idzigwira ntchito izi:

- Kutsogolera kupanga ndondomeko za mmene ntchito za msamuko ziyendere.
- Kuwonetsetsa kuti chilungamo chikutsatidwa pogawa chipuputa misonzi.
- Kuthandizira ntchito ya msamuko kuti yiyende bwino.
- Kulandira madandaulo okhudza msamuko.
- Kupereka madandaulo a msamuko kwa oyenera.

### 2.3.3. Kasanjidwe ka misonkhano

Komiti idzikumana pakakhala kufunikira kutero.

### 2.3.4. Nthawi yokhala pa udindo

Anthuwa adzikhala pa udindowu kufikira ntchito zonse zokhudza msamuko ndi chipuputa misonzi zitatha.

## 2.4. MFUNDO ZOMWE KOMITI YOTHANA NDI MADANDAULO A OGWIRA NTCHITO (WGRMC) IDZITSATA

Komitiyi idzikhala yoyamba kulandira madandaulo a ogwira ntchito okhudzidwa ndi Pulogalamu ya RCRP-2. Madandaulo amenewa ndi okhudza ogwira ntchito m'dera lokhudzidwa ndi pulogalamuyi. Oyimira ogwira ntchito adzisankhana ndipo ena mwa memembala akuyenera kukhala akazi ndipo chiwerengero chawo chisachepere 40 pa anthu 100 alionse. Mamembala a komitiyi ayenera kugwira ntchito mwaufulu ndi mopanda mantha. Wapampando adzisankhidwa kuchokera mwa oyimira ogwira ntchito, ndipo mlembi ayenera kukhala m'modzi mwa opereka upangiri amene amakhala oyang'anira ntchito mmalo mwa Boma. Nthawi yothetsera madandaulo ndi sabata ziwiri . Komiti imeneyi idzikhazikitsidwa ndi k ontirakita mmalo onse momwe muli ntchito za zomangamanga.

### 2.4.1. Oyenera kukhala membala wa (WGRMC)

Mamembala a komitiyi adzikhala ogwira ntchito, ma consultant, ma engineer a zomangamanga, mwa ena ndipo akuyembekezeka kutenga magawo awa:

1. Mkhalapampando.
2. Wachiwiri kwa mkhalapampando.
3. Mlembi.
4. Wachiwiri kwa mlembi.
5. Mlangizi woona kuti pasakhale kusiyana pakati pa amayi ndi abambo wochokera ku khonsolo.
6. Mlangizi woyangánira za ntchito pa khonsolo.
7. Woyimira amayi.
8. Woyimira abambo.
9. Woimira ogwira ntchito amene ali ndi ulumali.
10. Oimira kampani ya zomangamanga.

### 2.4.2. Ntchito ndi maudindo a komiti yolandira madandaulo a ogwira ntchito

Komitiyi idzikhala yoyamba kulandira madandaulo komanso nkhawa za ogwira ntchito ndipo idzigwira ntchito izi:

- Kuchita misonkhano yodziwitsa kapena yozindikirikitsa ogwira ntchito mogwirizana ndi makomiti a'mdera/

paboma/m'mimzinda.

- Kuonetsetsa kuti bokosi la madandaulo liri malo ofikirika mosavuta kwa aliyense komanso otetezeka.
- Kutsegula bokosi la madandaulo pakatha sabata ziwiri zirizonse.
- Kulemba madandaulo onse omwe alandiridwa.
- Kuwunika komanso kusanthula madandaulo onse amene alandir idwa ndi kuchotsa onse omwe sakukhudzana ndi pulogalamuyi.
- Kuonetsetsa kuti ntchito yothana ndi madaundolo ikuchitika mwachilungamo komanso poyera.
- Kufufuza ndi kuthandizira kuthetsa madandaulo.
- Kumvetsera ndi kulandula madandaulo kapena milandu yonse yoperekedwa ndi anthu kapena onse okhudzidwa ndi pulogalamu.
- Kuonetsetsa kuti ndondomeko zothandizira chitetezo, zofunika pa ntchito, maufulu achibadwidwe a anthu, kutukuka pa chuma, ulumali, kusasiyana pakati pa amayi ndi abambo, ntchito za zachilengedwe ndi umoyo zikutsatidwa pomwe Pulogalamu ya RCRP-2 ikugwirika komanso ikadzatha.
- Kusunga mbiri ya momwe madandaulo aliri komanso momwe athetsedwera.
- Kutumiza milandu yokhudza ndi nkhanza za pakati pa amayi ndi abambo (monga zomenyana, kugwilirira, ndi zina zotero) ndi milandu ina yaupandu kwa adindo oyenelera kuti akachitepo kanthu.
- Kutumiza madandaulo omwe sangathe kuthana nawo ku makomiti a'mdera/paboma/mmizinda kuti achitepo kanthu.
- Kudziwitsa odandaula za mmene madandaulo awo akuthandizikira.
- Kukonza malipoti a momwe madandaulo akuyendera ndi kuwapereka ku makomiti a mdera/paboma/mmizinda (pamisonkhano ya pamwezi).

### 2.4.3. Dongosolo la misonkhano

Komiti idzichita misonkhano mwezi uliwonse ngati ntchito za RCRP-2 zikuchitika. Komiti itha kusintha kuchuluka kwa misonkhano malinga ndi mmene madandaulo akuperekedwera.

### 2.4.4. Ndondomeko za misonkhano

Kontirakita adzithandizira kusankha wapampando wa WGRMC kuchokera mwa mamembala ake.

- Wapampando wa komiti ndi yemwe adzitsogolera misonkhano ndipo adzionetsetsa kuti ikuchitika mwadongosolo komanso motsata malamulo a komiti nthawi zonse. Ngati wapampando palibe, munthu wina ogwirizira wapampando adzitsogolera msokhanowu.
- Mlembi wa komiti ndi yemwe adziitanitsa misonkhano, kulembera zokambirana za misonkhanoyo (minutes), kugawa ndi kusunga zolembedwa zosayinira.
- Kuti msonkhano ukhale ovomerezeka, payenera kukhala mamembala a komiti osachepera theka.
- Komiti idzitsatira mfundo zolimbikitsa kuchita zinthu poyera komanso mwachilungamo nthawi zonse.
- Kuonetsetsa kuti ndondomeko zothandizira chitetezo, zofunika pa ntchito, maufulu achibadwidwe a anthu, kutukuka pa chuma, za ulumali, kusasiyana pakati pa amayi ndi abambo, ntchito zachilengedwe ndi umoyo zikutsatidwa pomwe Pulogalamu ya RCRP-2 ikugwirika komanso ikadzatha.
- Kutengera ndi dandaulo kapena mlandu, odandaulo omwe akukhudzidwa ndi Pulogalamu adzipemphedwa kukaonekera kubwalo lomva dandaulo kapena mlandu

wake. Ngakhale izi ziri chonchi, odandaula sakuloledwa kukhalapo pa milandu ina monga ya madandaulo okhudza amayi ndi abambo, komanso kugonana. Madandaulo otere adzatumizidwa ku bungwe lapadera lothandizira kugwira ntchito zimenezi pansi pa RCRP-2.

### 2.4.5. Malo ochitira misonkhano

Komiti idzichititsa misonkhano yake pa malo omwe ali pafupi ndi mamembala ake.

### 2.4.6. Kufalitsa zotsatira za dandaulo kapena mlandu

Komitiyi idzidziwitsa zotsatira za chigamulo chake kwa makomiti a m'dera/paboma/mmizinda mkati mwa masiku asanu ndi awiri (7) kuchokera tsiku lomwe adagwirizana za chigamulo.

### 2.4.7. Katumizidwe ka malipoti

- Komitiyi idzipereka malipoti ake kwa kontirakita komanso ma office woyendetsa pulogalamuyi.
- Komitiyi idzigwira ntchito limodzi ndi makomiti a m'dera/paboma/mmizinda pa nkhani zonse zomwe zatumphuka komanso mmene madandaulo akuyendetsedwera.
- Komitiyi idzilumikizananso ndi makomiti omwe akuyendetsa Pulogalamu ngati kuli kofunika kutero.

### 2.4.8. Nthawi yokhala pa udindo

Mamembala a komiti adzikhala m'maundindo mu nthawi yonse yomwe pulogalamuyi ikutumikira.

## 2.5. MFUNDO ZOMWE KOMITI YOMVETSERA NDI KUTHANA NDI MADANDAULO YA M'DERA (AGRMC) IDZITSATA

Komitiyi idzikhazikitsidwa m'dera la mfumu yandodo (TA) komwe ntchito za pansi pa Pulogalamu ya RCPR-2 ikugwirika. Mafumu kapena andale sakuloledwa kukhala mamembala a komitiyi. Mafumu a ku madera akhala olangiza komanso owunikira zinthu zina chabe koma osati kukhala mamembala a komitiyi. Komitiyi ikuyenera kudziwitsa mafumu za madandaulo omwe yalandira kuti mafumuwo ayithandize mu njira zina. Komitiyi ikuyenera kuthana ndi madandaulo pasanathe sabata ziwiri chilandilireni madandaulowo.

### 2.5.1. Kapangidwe ka komiti ya m'mudzi yoyang'anira madandaulo (AGRMC)

Komitiyi ikhala ndi mamembala enieni a ku madera, kuphatikizipo ogwira ntchito za boma okhudzika ndi Pulogalamu mmaderawo kapena kufupi ndi deralo komanso oyimira makomiti ena a m'dera. Komitiyi idzisankha munthu mmodzi yemwe ndi membala wa komiti yachitukuko yadera (ADC) kukhala w apampando. Mlembi wa komitiyo adzikhala wogwira ntchito za boma . Mamembala osankhidwa mukomitiyi adziyenera kukhala okhulupilirika komanso a mbiri zabwino. Amayi osachepera 40 pa anthu 100 alionse ayenera kukhala mamembala a komitiyi. Akatswiri ena adzisankhidwa ngati pakufunika kutero. Komiti ya m'boma ya DGRMC idzithandizira zisankho za wapampando ndi mlembi omwe adzitumikira m'maudindo awo kwa zaka zonse za pulogalamuyi.

Tsatanetsatane wa mamembala a komiti ya mfumu yandodo (AGRMC):

1. Oyimira anthu omwe akupindula ndi Pulogalamu m'deralo.
2. Mlangizi wa boma m'deralo (yemwe akukhudzidwa kwambiri ndi Pulogalamu) – Mlembi;
3. Oyimira azipembedzo.
4. Oyimira komiti yadera la mfumu yandodo.
5. Oyimira komiti yowona za ngozi zogwa mwadzidzi (DRM),
6. Oyimira anthu a ulumali.
7. Oyimira achinyamata (ochokera ku gulu

5 This shall only operate under district councils

kapena bungwe lililonse la achinyamata m'deralo).

8. Oyimira amayi (ochokera ku magulu kapena mabungwe a amayi m'deralo).
9. Oyimira komiti yachitukuko yam'mudzi – Wapampando.
10. Oyimira bungwe la m'dera (Community-Based Organization).
11. Oyimira gulu lachitetezo m'dera.
12. Oyimira komiti ya m'dera lomwe likukhudzidwa ndi Pulogalamu.
13. Oyimira komiti yoona za malo kapena alembi a malo.
14. Oyimira mabungwe omwe si aboma (kuphatikizapo CBOs).

### 2.5.2. Ntchito ndi maudindo a komiti ya ku dera la mfumu yandodo (AGRMC)

Komitiyi idzikhala yoyambirira kulandira madandaulo ochokera ku makomiti a m'dera/ogwira ntchito zokhudzana ndi Pulogalamu ya RCRP-2 m'deralo. Izi ndi zina mwa ntchito zake:

- Kuchita misonkhano yodziwitsa kapena yozindikirikitsa ogwira ntchito limodzi ndi komiti ya pa boma.
- Kulandira ndi kusunga mbiri ya madandaulo ochokera kwa okhudzidwa ndi Pulogalamu.
- Kufufuza ndi kuthandizira kuthetsa madandaulo.
- Kuunika madandaulo omwe alandiridwa.
- Kumva ndi kulandula milandu yomwe yalandiridwa.
- Kusunga mbiri ya momwe madandaulo aliri komanso momwe athetsedwera.
- Kulandira madandaulo kapena milandu yochokera ku makomiti a m'dera/kwa ogwira ntchito ndi kudziwitsa mmene athetsedwera.
- Kutumiza madandaulo omwe akanika kuthana nawo ku komiti ya pa boma kuti ichitepo kanthu.
- Kutumiza milandu yokhudza nkhanza za pakati pa amayi ndi abambo (monga zomenyana, kugwilirira, ndi zina zotero) ndi milandu ina yaupandu kwa adindo oyenelera kuti akachitepo kanthu.
- Kudziwitsa odandaula za mmene madandaulo awo ayankhidwira.
- Kutumiza malipoti apa mwezi ku komiti ya pa boma komanso kudziwitsa mafumu am'deralo za malipotiwo .

### 2.5.3. Kasanjidwe ka misonkhano

Komiti idzichita misonkhano mwezi uliwonse ku malo komwe Pulogalamu ya RCRP-2 ikuchitika monga pa malo omwe pakuchitika ntchito ya zomangamanga kapena ku ofesi ya komiti yachitukuko ya m'dera la mfumu yandodo. Komitiyi idzitha kusintha kuchuluka kwa misonkhano yake malinga ndi momwe madandaulo akufikira. Madandaulo ena adzifunika kuthana nawo mwachangu popanda kudikira nthawi ya misonkhano yokhazikika. Madandaulo awa akukhudza nkhani za nkhanza pakati pa amayi ndi abambo, kuchita kapena kuyankhula zokhudza zogonana popanda chilolezo/chivomerezo komanso milandu yaupandu.

### 2.5.4. Ndondomeko za misonkhano

- Wapampando wa komiti ndi ymwee adzitsogolera misonkhano ndipo adzaonetsetsa kuti ikuchitika mwadongosolo komanso kuti motsata malamulo a komiti nthawi zonse. Ngati wapampando palibe, munthu wina ogwirizira wapampando adzatsogolera msokhanowu.
- Mlembi wa komiti ndi amene adziitanitsa misonkhano, kulembera zokambirana za misonkhanoyo, kugawa ndi kusunga zolembedwa zosayiniridwa.
- Chiwerengero choyenera chovomerezeka

kuti msonkhano wakomiti uchitike (quorum) chidzayenera kukhala mamembala osachepera theka ndi m'modzi (50 pelesenti kuphatikizirapo mmodzi) mwa mamembala oyenera kupezeka.

- Komiti idzitsatira mfundo zolimbikitsa kuchita zinthu poyera komanso mwachilungamo nthawi zonse.
- Kutengera ndi dandaulo kapena mlandu, odandaula omwe akukhudzidwa ndi Pulogalamu adzipemphedwa kukaonekera kubwalo lomva dandaulo kapena mlandu wawo. Ngakhale izi ziri chonchi, odandaula sadziloledwa kukhalapo pa milandu ina monga ya umbanda. Madandaulo okhudza amayi ndi abambo komanso kugonana, adzatumizidwa ku bungwe lapadera lothandizira kugwira ntchito zimenezi pansi pa RCRP-2

### 2.5.5. Malo ochitira misonkhano

- Komiti idzichititsa misonkhano yake pa malo omwe ali oyenelera kwa iyo komanso a pafupi ndi mamembala ake ku dera komwe ntchito ya zomangamanga ikuchitikira.
- Komitiyi idziyendera malo omwe kukumangidwa ngati kuli kofunikira kutero.
- Kufalitsa zotsatira za madandaulo.
- Komitiyi idzifotokozera odandaula zotsatira za madandaulo awo mkati mwa masiku asanu ndi awiri (7) ogwira ntchito kuchokera tsiku lomwe komitiyi yapereka chiganizo chake.

### 2.5.6. Zofunikira popereka malipoti

- Komitiyi idzipereka malipoti ake ku komiti ya pa boma.
- Komitiyi idzigwira ntchito limodzi ndi komiti ya pa boma pa nkhani zonse zomwe zatumphuka komanso mmene madandaulo akuyankhidwira.
- Komitiyi idzikhala ikugwirizana ndi ma komiti kapena maofesi a mapulogalamu ena ngati pakufunikira kutero.

## 2.6. MFUNDO ZOMWE MAKOMITI OTHANA NDI MADANDAULO A PA BOMA NDI MMIZINDA IDZITSATA

Makomitiwa adzikhala oyambirira kulandira madandaulo ochokera kwa okhudzidwa ndi Pulogalamu ya RCRP-2 komanso ochokera ku makomiti a m'dera la mfumu yandodo, mu wodi komanso kwa ogwira ntchito . Makomitiwa adzikhala oyambirira kulandira milandu kapena bwalo lomva milandu la apilo yokhudzana ndi Pulogalamu ya RCRP-2. Nthawi yothetsera madandaulo ndi masiku 14. Ngati odandaula sadakhutire, nkhaniyo idzatumizidwa ku komiti ya dziko yothetsa madandaulo .

### 2.6.1. Mamembala a komiti ya pa boma

Mamembala a komitiyi adzikhala motere:

1. DMkulu wokonza mapulani ndi chitukuko – Wapampando.
2. Mkulu woyang'anira zachilengedwe pa boma.
3. Mkulu wa zamalo pa boma.
4. Mkulu woona za ngozi zogwa mwadzidzidzi pa boma – Mlembi
5. Mkulu woyang'anira chitukuko cha m'madera.
6. Mkulu woona kuti pasakhale kusiyana pakati pa amayi ndi abambo pa boma.
7. Mkulu woyang'anira za ntchito pa boma.
8. Mkulu woyang'anira zachisamaliro cha anthu pa boma.
9. Mabwalo oweruza milandu/Majisitiliti.
10. Mkulu wa zofalitsa nkhani pa boma.
11. Mkulu woyang'anira za malo pa boma.
12. Woyimira apolisi – Ofesi yothandiza ochitiridwa nkhanza.

13. Woyimira mabungwe omwe si aboma.

### 2.6.2. Mamembala a komiti ya mumzinda/m'matauni

Adzikhala motere:

1. Mkulu wokonza mapulani ndi chitukuko – Wapampando
2. Mkulu woyang'anira zachilengedwe.
3. Mkulu woona za malo.
4. Mkulu woona za ngozi zogwa mwadzidzidzi – Mlembi
5. Mkulu woyang'anira chitukuko cha mmatawuni.
6. Mkulu woona kuti pasakhale kusiyana pakati pa amayi ndi abambo.
7. Mkulu woyang'anira zachisamaliro cha anthu.
8. Woyimira apolisi – Ofesi yothandiza ochitiridwa nkhanza.
9. Woyimira mabungwe omwe si aboma.
10. Mabwalo oweruza milandu.
11. Mkulu wa zofalitsa nkhani.

### 2.6.3 Ntchito ndi maudindo a komiti yolandira madandaulo pa boma ndi mmizinda

Ntchito ndi maudindo a makomiti amenewa ziri motere:

- Kuthandiza kukhazikitsa makomiti a m' dera la mfumu yadera, ndi mu wodi.
- Kuthandizira maphunziro ndi misonkhano yodziwitsa anthu ndondomeko zothetsera madandaulo okhudza Pulogalamu ya RCRP-2.
- Kulemba mbiri (record) ya madandaulo onse ochokera kwa odandaula.
- Ku unikanso madandaulo onse ochokera ku makomiti a mdera la mfumu yandodo kapena makomiti am'dera, ndi wodi.
- Kufufuza komanso kuthandizira kupeza njira zothetsera madandaulo.
- Kulondoloza milandu kapena madandaulo komanso kudziwitsa makomiti a mmadera onse, komanso anthu opsinjika.
- Kuonetsetsa kuti ntchito zonse zogwirika pansi pa Pulogalamu ya RCRP-2 zikuchitika poyera komanso mwachilungamo.
- Kuonetsetsa kuti ndondomeko zothandizira chitetezo, zofunika pa ntchito, maufulu achibadwidwe a anthu, kutukuka pa chuma, za ulumali, kusasiyana pakati pa amayi ndi abambo, ntchito zachilengedwe ndi umoyo zikutsatidwa pomwe Pulogalamu ya RCRP-2 ikugwirika komanso ikadzatha.
- Kuunika madandaulo onse olandiridwa pa (mwezi).
- Kutumiza madandaulo omwe sadathetsedwe ku komiti ya GRMC pansi pa Pulogalamu ya RCRP-2 kuti achitepo kanthu.
- Kutumiza milandu yokhudza nkhanza za pakati pa amayi ndi abambo (monga zomenyana, kugwirilira, ndi zina zotero) ndi milandu ina yaupandu kwa adindo oyenelera kuti achitepo kanthu.
- Kukonza malipoti a momwe madandaulo akuyendetseredwa ndi kukawapereka ku makomiti a mmakhonsolo pa misonkhano yochitika pa miyezi itatu iliyonse pa chaka.
- Kuyang'anira, kuchita kalondolondo ndi kuunika mmene makomiti a AGRMC, CGRMC/Ward GRMC akugwirira ntchito.
- Kuyendera malo omwe kukugwiridwa ntchito za Pulogalamu ya RCRP-2 kanayi pa chaka pofuna kuona mmene makomiti a mdera, ku dera la mfumu yandodo ndi mu wodi akugwilira ntchito.
- Kupereka malipoti kanayi pa chaka ku

komiti yoona za madandaulo m'dziko, komanso mu makhonsolo okhudza ntchito za makomiti a madandaulo.

- Kuchita kalondolondo ngati malamulo komanso zigamulo za makomiti osiyanasiyana zikutsatidwa.

### 2.6.4 Kasanjidwe ka Misonkhano

Komitiyi idzikhala ndi misonkhano yake kanayi pachaka. Komitiyi itha kusintha nthawi ya misonkhano yake malinga ndi mmene madandaulo olandiridwa ku makomiti a m'dera aliri.

### 2.6.5 Ndondomeko ya Misonkhano

- Mkulu wokonza mapulani ndi chitukuko adzikhala wapampando wa komiti, ndipo mkulu woyang'anira chilengedwe pa boma kapena mu mzinda adzikhala mlembi.
- Wapampando wa komiti ndi yemwe adzitsogolera misonkhano ndipo adziwonetsetsa kuti ikuchitika mwadongosolo komanso kuti malamulo a komiti akutsatidwa nthawi zonse. Ngati wapampando palibe, munthu wina ogwirizira udindo wa wapampando adzitsogolera msonkhanowu.
- Mlembi wa komiti ndi yemwe adziitanitsa misonkhano, kulembera zokambirana za misonkhanoyo , kusayinitsa, komanso kugawa ndi kusunga.
- Chiwerengero choyenera chovomerezeka kuti msonkhano wakomiti uchitike chidziyenera kukhala mamembala oposa theka .
- Komiti idzitsatira mfundo zolimbikitsa kuchita zinthu poyera komanso mwachilungamo nthawi zonse.
- Kuonetsetsa kuti ndondomeko zothandizira chitetezo, zofunika pa ntchito, maufulu achibadwidwe a anthu, kutukuka pa chuma, za ulumali, kusasiyana pakati pa amayi ndi abambo, ntchito za zachilengedwe ndi umoyo zikutsatidwa pamene Pulogalamu ya RCRP-2 ikugwirika komanso ikadzatha.
- Kutengera ndi dandaulo kapena mlandu, odandaula omwe akukhudzidwa ndi Pulogalamuyi adzipemphedwa kukaonekera ku bwalo lomva madandaulo kapena mlandu wawo. Ngakhale izi ziri chonchi, odandaulaa sadzaloledwa kukhalapo pa milandu ina monga ya umbanda. Madandaulo okhudza amayi ndi abambo komanso kugonana, adzatumizidwa ku bungwe lapadera lothanndizira kugwira ntchito zimenezi pansi pa RCRP-2.

### 2.6.6 Malo Ochitira Misonkhano

Komitiyi idzichitira misonkhano yake pamalo a pa boma kapena mu mzinda. Komitiyi idziyendera malo omwe kukumangidwa ngati kuli kofunikira kutero.

### 2.6.7 Kufalitsa zotsatira za madandaulo

Komitiyi idzifotokozera makomiti a mmakhonsolo za ziganizo zake pa madandaulo mkati mwa masiku asanu ndi awiri (7) kuchokera pa tsiku lomwe komitiyi yapanga chiganizo.

### 2.6.8 Zofunikira mu malipoti

Makomiti a pa khonsolo adzipereka malipoti okhudza nkhani zonse zomwe zatumphuka komanso mmene milandu ikuyendera ku makumiti akuluakulu a pa khonsolo ndi ku ma ofesi woyendetsa pulogalamu ya RCRP – 2.

## 2.7 NTCHITO ZA KOMITI YOTHETSA MADANDAULO YA DZIKO LONSE (NGRMC)

Iyi ndi komiti yadziko lonse ndipo idzimva milandu yochokera kwa okhudzidwa ndi Pulogalamu ya RCRP-2 yomwe makomiti aang'ono ayitumizira. Komitiyi idziyenera kuthetsa madandaulo omwe yalandira m'masiku 21. Ngati odandaula wakhutitsidwa ndi chigamulo, nkhaniyo idzatsekedwa. Koma ngati odandaula sadakhutitsidwe ndipo kuti nkhaniyo sinatsekedwe ndi NGRMC, odandulayo adzalangizidwa kukasuma

ku mabwalo a milandu kapena ku ofesi ya mtetezi wa anthu komwe kudzadzaperekedwe chigamulo.

### 2.7.1 Mamembala a komiti ya NGRMC

Komitiyi idzikhala ndi mamembala ochokera ku maunduna ndi nthambi za boma komanso oyendetsa pulogalamu ya RCRP-2. Mamembala a NGRMC adzakhala motere:

1. Woyang'anira Pulogalamuyi – Wapampando.
2. Akatswiri owona zachilengedwe mu pulogalamuyi.
3. Akatswiri owona za chitetezo, chikhalidwe ndi umoyo wa anthu mu pulogalamuyi – Mlembi.
4. Woyimira Unduna owona za malo, nyumba ndi chitukuko cha m'tawuni.
5. Woyimira nthambi ya boma yoona za chilengedwe.
6. Woyimira nthambi yoteteza malo.
7. Woyimira unduna wa za ntchito.
8. Woyimira unduna woona kuti pasakhale kusiyana pakati pa amayi ndi abambo, ana ndi chisamaliro cha anthu.
9. Katswiri wa kauniuni ndi kalondolondo wa pulogalamuyi.
10. Katswiri wa zofalitsa mauthenga m'pulogalamuyi.
11. Woyimira mabwalo oweruza milandu.
12. Woyimira ofesi yomva madandaulo (ombudsman).

### 2.7.2 Ntchito ndi maudindo a komiti ya m'dziko yolandira ndi kuthetsera madandaulo (NGRMC)

Ntchito ndi maudindo a komitiyi ziri motere:

- Kuonetsetsa kuti ntchito zomwe zikugwiridwa mu Pulogalamu ya RCRP-2 zikuchitika mwachilungamo komanso poyera.
- Kulemba madandaulo onse omwe alandiridwa.
- Kuunika madandaulo ochokera ku makomiti a mmakhonsolo.
- Kufufuza ndi kuthandizira kuthetsa madandaulo.
- Kutumiza ku mabwalo a milandu nkhani zomwe mayankho ake sadapezeke.
- Kutumiza milandu yokhudzana ndi nkhanza pakati pa amayi ndi abambo (monga zomenyana, kugwilirira, ndi zina zotero) ndi milandu ina yaupandu kwa adindo oyenelera kuti achitepo kanthu.
- Kudziwitsa makomiti a mmakhonsolo za madandaulo omwe alandiridwa.
- Kuunika madandaulo ochokera mmakhonsolo kanayi pachaka ndikupereka upangiri ku makhonsolo ndi mabungwe oyenelera.
- Kukonza malipoti a dziko lonse a kathetsedwe ka madandaulo ndikuwapereka ku mabungwe ndi magulu oyenelera pa misonkhano ya panthawi.
- Kuchititsa maphunziro othandizira ukadaulo wa makomiti a mmakhonsolo.
- Kuona komanso kuunika ngati makomiti olandira ndikuthetsa madandaulo akugwira ntchito moyenelera.
- Kuchita kalondolondo ngati malamulo ndi zigamulo za makomiti osiyanasiyana zikutsatiridwa.

### 2.7.3 Kakonzedwe ka mikumano

Komitiyi idzi khala ndi mikumano yake kanayi pachaka koma itha kusintha nthawi ya mikumano yake malinga ndi mmene madandaulo abwelera kuchokera ku ma khonsolo.

### 2.7.4 Ndondomeko ya mikumano

- Wapampando wa komiti ndi yemwe adzitsogolera zokambirana mmikumano

ndipo adzionetsetsa kuti ikuchitika mwadongosolo komanso motsata malamulo nthawi zonse. Ngati wapampando palibe, munthu wina ogwirizira udindo wa wapampando adzitsogolera mkumanowu.

- Mlembi wa komiti ndi yemwe adzilemba zokambiarana zonse pa mikumanoyi ndikuonetsetsa kuti zokambiranazi zagawidwa kwa mamembala onse komanso zasungidwa poyenera.
- Chiwerengero chovomerezeka kuti mkumano uchitike chiyenera kukhala ma membala oposera theka.
- Komiti idzitsatira mfundo zolimbikitsa kuchita zinthu poyera komanso mwachilungamo nthawi zonse.
- Kutengera ndi dandaulo kapena mlandu, odandaula omwe akukhudzidwa ndi Pulogalamu adzapemphedwa kukaonekera ku bwalo lomva dandaulo kapena mlandu wawo. Ngakhale izi ziri chonchi, odandaula adzadziwitsidwa kuti asakhalepo mu zokambirana zina ndi a komiti.

### 2.7.5 Malo ochitira mikumano

Komitiyi idzichitira mikumano yake ku ofesi yayikulu ya RCRP-2. Ngakhale izi ziri chonchi, komitiyi itha kusankha kuchitira mikumano yake ku malo ena ngati kuli kofunikira kutero. Mikumano ina ya komitiyi itha kumachitika kudzera pa makina a intaneti. Komitiyi idzithanso kuyendera makhonsolo komanso malo omwe ntchito ya zomangamanga zikuchitikira ngati kuli kofunikira kutero.

### 2.7.6 Kufalitsa zotsatira za mikumano

Komitiyi idzifotokozera za chigamulo chake kwa odandaula pasanathe masiku asanu ndi awiri.

### 2.7.7 Zofunikira mu malipoti

Komitiyi idzipereka malipoti okhudza nkhani zonse zomwe zalandiridwa komanso mmene ntchito zonse zothana ndi madandaulo zikuyendera ku komiti ya akuluakulu a nthambi za Boma komanso magulu ena okhudzidwa.

### 2.7.8 Nthawi yokhala pa udindo


Komitiyi idzikhala ikugwira ntchito kufikira pomwe Pulogalamu RCRP-2 idzathere.

# 3 NJIRA ZOLANDILIRA NDI KUTHETSERA MADANDAULO

Njira Zolandilira ndi kuthestsera ziri mmagawo asanu motere:

1. Kulandira madandaulo.
2. Kuunika, kusanthula ndi kuyankha.
3. Kuthetsa ndi kutseka nkhani.
4. Kulembera ndi kuunika mmene zayendera.
5. Kuunika momwe ndondomeko Yolandilira ndi Kuthetsera Madandaulo ikugwirira ntchito.

**CHITHUNZI CHACHIWIRI: MAGAWO ASANU A NDONDOMEKO YA KALANDIRIDWE NDI KATHETSEDWE KA MADANDAULO**




## 3.1 GAWO LOYAMBA: KULANDIRA MADANDAULO

Odandaula onse adzipereka madandaulo awo ku makomiti a m'dera komanso mu wodi yawo (CGRMC/Ward GRMC) omwe akhazikitsidwa ndi Pulogalamu ya RCRP-2. Madandaulo atha kuperekedwa munjira zosiyanasiyana monga izi:

**Kupereka madandaulo kwa a komiti:** Izi zidzichitika poyankhula kapena kulemba madandaulo omwe akuperekedwa nthawi imene mamembala a komiti akukumana kapena pamene pali mikumano ndi akuluakulu oyendetsa pulogalamu komanso magulu ena a m'madera nthawi iliyonse.

**Bokosi la madandaulo:** Mabokosi a madandaulo adziikidwa m'malo oyenelera monga m'madera omwe ntchito za zomangamanga zikugwiridwa, komwe okhudzidwa ndi Pulogalamu ya RCRP-2 atha kumatulako madandaulo awo nthawi iliyonse.

**Njira zina:** Uthenga wa pafoni yammanja (SMS), zikalata za chinsinsi, nambala za foni zoimba mwaulere (351).

Posatengera njira za momwe dandaulo laperekedwera, makomiti a CGRMC/Ward GRMC adzilemba madandaulo onse m'mabuku komanso mmafomu omwe adzipatsidwa. Madandaulo adzi tumizidwa ku makomiti AGRMC/City GRMC ngati sanakakwanitsidwe kuthetsedwa ndi komiti ya ku dera. Nthawi zina, odandaula atha kufuna kusapereka madandaulo ku makomiti a kudera (CGRMC/Ward GRMC) chifukwa cha kusamvetsetsana kapena kuti odandaulidwayo ndi wa m'dera lomwelo. Panthawiyi, makomiti a pa boma/mzinda adzigwirizana za mmene angathetsere madandaulo koma makomiti a ku dera ndi omwe adzipatsidwa mpata oyambirira kumva madandaulo.

Ogwira ntchito mu Pulogalamu ya RCRP- 2 adziperekamadandauloawokukomitiYolandirandi Kuthetsa Madandaulo a ogwira ntchito (WGRMC). Komiti ya WGRMC idzilemba madandaulo onse mkaundula ndi fomu yolembamo madandaulo a ogwira ntchito. Madandaulo adzitumizidwa kwa kontirakita ndi ma ofesi oyendetsa Pulogalamu ya RCRP-2 pokhapokha ngati komiti ya WGRMC yalephera kuthana ndi madandaulo omwe inapatsidwa.

## 3.2 GAWO LACHIWIRI: KUUNIKA, KUSANTHULA NDI KUYANKHA

Pamene dandaulo laperekedwa, makomiti a ku (CGRMC/Ward GRMC) akuyenera kupereka yankho la madandaulo pasanadutse masabata awiri (masiku 14). Cholinga cha ganizoli ndikuonetsetsa kuti madandaulo akuthetsedwa mwachangu. Pamene dandaulo laperekedwa, makomiti a (CGRMC/Ward GRMC kapena WGRMC adzaunika ngati madandaulowo akugwirizana ndi ntchito za mu Pulogalamu ya RCRP-2 Ngati madandaulo sakukhudzana ndi Pulogalamu ya RCRP 2, odandaulayo adzilangizidwa kuti akapereke madandaulo ake ku mabungwe oyenera.

Pamene madandaulo akugwirizana ndi ntchito za Pulogalamu ya RCRP-2, makomiti a CGRMC/Ward GRMC ndi WGRMC akuyenera kuchita kafukufuku kuti apeze zoona zenizeni za madandaulowo. Zotsatira zake zidziperekedwa kwa odandaula.




Figure 2: Mkumano wofuna maganizo akuluakulu akukhosolo pa bukhu la madando-Nkhotakota

## 3.3 GAWO LACHITATU: KUTHETSA NDI KUTSEKA NKHANI

Pomwe chigamulo chaperekedwe ndipo wodandaula wagwirizana nacho, wodandaulayo adziyenera kusayinira mu buku la madandulo kapena mu fomu Yolandilira ndi Kuthetsera Madandaulo. Izi zikutsimikizira kutsekedwa kwa dandaulo. Mamembala awiri a makomiti a CGRMC/Ward GRMC kapena WGRMC (makamaka Wapampando ndi Mlembi) adziyenera kusayinira ngati madandulo akukhudza anthu omwe akuwatumikira. Izi zidzisonyeza kuti dandaulo limene linaperekedwa launikidwa ndipo latsekedwa.

## 3.4 GAWO LACHINAYI: BUKU LA MADANDAULO

Madandaulo onse amene adziperekedwa adzilembedwa mu kaundula kapena mu buku limene anthu atha kulipeza mosavuta ndipo bukuli lidzisungidwa ndi a makomiti. Mabuku olembamo madandaulo a makomiti a kudera komanso ogwira ntchito adzikhala atatu. Ngati dandaulo liri lokhudza nkhanza za pakati pa amayi ndi abambo komanso kugonana, dandaulolo lidzilembedwa osatchula dzina lenileni. Pa dandaulo lililonse lomwe launikidwa, latsekedwa kapena latumizidwa kwina, buku kapena fomu imodzi ya dandaulo lidzitumizidwa ku makomiti ena kuti akasunge mu kaundula osungiramo mbiri za madandaulo monga:CGRMC/Ward GRMC, AGRMC, DGRMC/City GRMC, ndi NGRMC kuti adzitha kulondoloza za mmene madandaulo anayendera. Izinso zidzithandiza kuti khonsolo ikhale ndi mbiri ya madandaulo onse omwe alandiridwa komanso kuthetsedwa m'bomalo ndi makomiti osiyana-siyana.


Pogwiritsa ntchito zimenezi, makhonsolo adzikwanitsa kukhala ndi mndandanda wa madandaulo komanso kupeza mayankho ake. Moonjezera, makhonsolo adzikwanitsa kulondoloza ngati zomwe adagwirizana zikuchitika.

## 3.5 GAWO LACHISANU: KUUNIKA MOMWE NDONDOMEKO YOLANDILIRA NDI KUTHETSERA MADANDAULO IKUGWIRIRA NTCHITO.

Kuunika momwe ndondomeko yolandilira ndi kuthetsera madandaulo ikugwirira ntchito kutha kuphatikizidwa ndi njira ina iliyonse yochitira kauniuni wa Pulogalamu ya RCRP-2. Izi zidzichitika pogwiritsa ntchito kaundula olembamo madandaulo mu Pulogalamuyi yemwe makhonsolo akusunga. Izi zidzithandiza kulondoloza ngati ndondomeko Yolandilira ndi Kuthetsera Madandaulo ndi yoyenera. Izi zidzithandiza kuonetsetsa ngati mfundo Zolandilira ndi Kuthetsera Madandaulo zikugwiritsidwa ntchito. Bungwe lapadera la kalondolondo lidziwunikiranso mmene ntchitoyi ikuyendera ndi kupereka mayankho.

Njira Yolandilira ndi Kuthetsera Madandauloyi idzithandizira kayendetsedwe kabwino ka Pulogalamu ya RCRP-2. Kuonjezera apo, njirayi idzithandizira kufufuza madandaulo komanso kukonza zinthu zotsamwitsa pa ndondomeko yoperekera madandaulolo mwamsanga. Njirayi idzithandiziranso kuthetsa madandaulo mwachilungamo ndi mwachangu, kuchepetsa milandu kuti isakule, kuteteza kuonongeka kwa chuma cha pulogalamuyi, komanso kuonetsetsa kuti onse okhudziwa ndi okhutira ndi kayendetsedwe ka RCRP-2.

**CHITHUNZI CHOONETSA KASANJIDWE KA MA OFESI OYENDETSA PULOGALAMU YA RCRP-2, NJIRA KOMANSO NDONDOMEKO ZOLANDILIRA NDI KUTHETSERA MADANDAULO (GRM)**



# 4 NJIRA ZINA ZOPELEKERA MADANDAULO NDI MALIPOTI



Figure 3: Mkumano wofunsa maganizo a anthu okhudzidwa ndi porojekiti pa bunkhu la madandaulo-Chidid, Nsanje

## 4.1. KUPEREKA MADANDAULO MWACHINDUNJI KU PULOGALAMU YA RCRP-2

Kuonjezera njira zina zomwe zafotokozeredwa mmwambamu, madandaulo ena atha kuperekedwa mwachindunji kwa Oyendetsa Pulogalamuyi (PCU). Aliyense okhudzidwa ndi Pulogalamuyi atha kupereka madandaulo mu njira za chinsisi kwa Wamkulu Oyendetsa Pulogalamuyi kapena kwa Akatswiri Oona Zachisamaliro Cha anthu. Oyendetsa Pologalamuyi, adzithandizira kupereka ndondomeko Zolandilira ndi Kuthetsera Madandaulo popereka mpata kwa onse okhudzidwa motsatira njira zoyenera.

Madandaulo ndi mayankho atha kuperekedwa m'chiyankhulo chilichonse chomwe chimayankhulidwa ndi anthu ambiri kudzera mu njira ngati izi:

- Aliyense atha kukadandaula ku maofesi oyendetsa Pulogalamu ya RCRP-2 omwe ali ku Lilongwe ku Area 12 moyang'anana ndi Wamkulu Palace.
- Kupereka madandaulo kudzera mmabokosi olandilira madandaulo omwe ayikidwa kumaofesi a RCRP-2 ku Lilongwe.
- Njira inanso ndi kudzera potumiza kalata ya madandaulo yomwe itha kulembedwa m'chiyankhulo chilichonse chomwe chimayankhulidwa ndi anthu ambiri ku Malawi kudzera ku ku keyala iyi:

NThe Project Coordinator, The Regional Climate Resilience Programme (RCRP-2),

P.O. Box 30136, Lilongwe 3, Malawi.

Kuimba foni pa nambala yaulere iyi: 351

Potumiza kalata ya madandaulo kudzera pa makina a Intaneti pa keyala iyi : grievances@rcrp.gov.mw.

Ngakhale pali njira zambiri zotumizira madandaulo ndi kulandilira mayankho, Pulogalamu ya RCRP-2 ikulimbikitsa odandaula onse kupereka madandaulo awo ku makomiti Olandira ndi Kuthetsa Madandaulo omwe ali nawo pafupi. Khumbo la Pulogalamu ya RCRP – 2 ndi kulimbikitsa kuti idzilandira madandaulo ndi kukwanitsa kupereka zotsatira za madanduolozo pasanathe masabata awiri (masiku 14).

## 4.2. KAFIKIRIDWE KA KOMITI YA MADANDAULO YA KU BANKI YAIKULU PA DZIKO LONSE

Pulogalamu ya RCRP-2 ikuthandizidwa ndi Banki Yayikulu pa Dziko Lonse (World Bank,) Bankiyi ilinso ndi njira yake Yolandlira ndi Kuthetsera Madandaulo ngati ndondomeko yosamalira anthu..

Wodandaula ali ndikuthekera kokapereka madandaulo ake kudzera mu makhothi ovomerezeka, kapena njira yomwe Bankiyi imatsatira . Wodandaula atha kuperekanso madandaulo ku Nthambi Yapadera Yolandira ndi Kuthetsera Madandaulo Ya Bankiyi (Independent Inspection Panel) kapena njira iliyonse yovomerezeka. Nthambi Yoyendetsa Pulogalamuyi (PIU) idzathandizira kuti madera okhudzidwa aphunzitsidwa bwino za Njira Yolandilira ndi Kuthetsera Madandaulo ya Banki Yayikuluyi. Nthambiyi idzafalitsa za njira yosavuta yolembetsera madandaulo, monga kulemba kalata.

Anthu omwe akukhulupira kuti ali ndi madandaulo okhudza ntchito za RCRP-2 kuchokera kwa anthu a m'mudzi kapena ogwira ntchito za pulogalamuyi, akhoza kupereka madandaulo awo polemba kalata kapena kuyimba foni ku Ofesi Yolandira ndi Kuthetsa Madandaulo ya Banki yayikuluyi ku Malawi.

Ndondomekoyi idzathandizira kuti madandaulo omwe alandiridwa awunikidwa mwachangu pofuna kuthetsa mavuto obwera chifukwa cha ntchito za pulogalamuyi. Anthu komanso madera omwe akhudzidwa ndi ntchito ya RCRP-2 akhoza kupeleka madandaulo awo ku Nthambi Yapadera Yolandira Ndikuthetsa Madandaulo Ya Bankiyi kudzera ku Ofesi ya Bungwe Yothandinza Ntchito Za Chitukuko ya ku Malawi. Zambiri za momwe okhudzidwawa adzaperekere madandaulo ku Njira Yolandilira ndi Kuthetsa Madandaulo ya Banki Yayikuluyi komanso Nthambi Yapadera Yolandira Ndikuthetsa Madandaulo Ya Bankiyi zidzafotokozedwa kwa anthu pa mikumano yosiyanasiyana.

Anthu onse okhudzidwa adzalimbikitsidwa Kuti aphunzire zambiri za momwe adziperekera madandaulo ku Njira Yolandilira ndi Kuthetsera Madandaulo ya Banki Yayikuluyi pa makina a intaneti kudzera ku keyala iyi : http://www.worldbank.org/GRS. komanso anthu okhudzidwa adzagwiritsanso ntchito keyala iyi popereka madandaulo ku Nthambi Yapadera Yolandira Ndikuthetsera Madandaulo Ya Bankiyi :www.inspectionpanel.org

Komabe, ngati madandaulowa ali aupandu, wodandaula adzaloledwa kufufuza chilungamo kudzera mu ndondomeko zoyenera zoperekera madandaulo za m'dziko la Malawi.

# 5 MADANDAULO APADERA

Pulogalamuyi ili ndi kuthekera kolandira mandaulo ena omwe angatchulidwe kuti ndi apadera. Madandaulo amenewa saadzithetsedwa ndi makomiti a mmadera Olandira ndi Kuthetsa Madandaulo. Makomiti Olandira ndi Kuthetsa Madandaulo a mmaderawa adzaphunzitsidwa za njira zoyenera zomwe angatsate polandira madandaulowa. Madandaulo a paderawa ndi monga;

## 5.1. MILANDU YAUPANDU

Milandu yonse yomwe yapezeka kuti ndi yaupandu ndi komiti Yolandira ndi Kuthetsa Madandaulo idziperekedwa ku Polisi mwachangu. Anthu adziphunzitdsiwa za mitundu ya milandu yotereyi ndikulimbikitsidwa kukanena za milanduyi ku Polisi.

## 5.2. KUGWIRITSA ANA NTCHITO ZOPOSA MISINKHU YAWO

Lamulo la Zantchito la mchaka cha 2000 (lounikidwaso mchaka cha 2022) limaletsa kulemba ntchito ana omwe sanakwanitse zaka 18. Lamuloli limaletsanso kugwiritsa ana ntchito zimene zingathe kuika miyoyo, maphunziro ndi kakulidwe kawo koyenera pachiopsezo. Mwachindunji, mchitidwewu ndi nkhanza kwa ana. Pulogalamu ya RCRP-2 siimavomereza mchitidwe wa nkhaza ina iliyonse. Makomiti Olandira ndi Kuthetsa Madandaulo Adziphunzitsa za mmene angaperekere ma l ipoti a nkhanza kwa adindo oyenera monga apolisi komanso alangizi a Zachisamaliro cha Anthu.

## 5.3. MTCHITIDWE OZEMBETSA ANA

Mchitidwewu ndi monga kugula kapena kuzembetsa ana ndi cholinga chofuna kukawagwiritsa ntchito zolakwika komanso zoposa misinkhu yawo. Kudzera mu Pulogalamu ya RCRP-2, ana osakwana zaka 18 atha kuzembetsedwa mmalo omwe Pulogal amuyi ikuchitikira ndi cholinga cholimbikitsa mchitidwe wogonana. Mchitidwe ngati uwu ndi mlandu waupandu, ndipo makomiti Olandilira ndi Kuthetsa Madandaulo a mmadera adziphunzitsidwa za mmene angadziwire ndi kutumiza madandaulo ngati awa kwa mabungwe ndi adindo oyenera.

## 5.4. NKHANZA ZA PAKATI PA AMAYI NDI ABAMBO NDI MCHITIDWE OKAKAMIZA KUGONANA

### 5.4.1. Tanthauzo la Nkhanza za Pakati pa Amayi ndi Abambo, Nkhanza Zogonana ndi Mawu Okhudza Zogonana

Tanthauzo la nkhanza za pakati pa amayi ndi abambo ndi mchitidwe osaloredwa omwe umayambitsidwa ndi munthu potengera kusiyana pa chibadwidwe kuti winayo ndi wamkazi kapena wamamuna. Mchitidwewu umabweretsa mavuto ku thupi, malingaliro ndi pa chuma. Nkhanza za pakati pa amayi kapena abambo ndi zoopya chifukwa zimaphwanya ufulu wachibadwidwe, kupereka chiopsezo pa umoyo ndi chitetezo cha munthu. Pokhazikitsa ndi kuyendetsa ntchito za Pulogalamu ya RCRP 2, patha kubwera madandaulo osiyanasiyana okhudza nkhanza zosiyanasiyana za pakati pa amayi ndi abambo. Zina mwa nkhanzazi ndi monga;

### 5.4.2. Nkhanza Zogonana

Izi ziri mgawo limodzi la nkhanza za pakati pa amayi ndi abambo zomwe zimalimbikitsa mchitidwe ogonana mosavomerezeka. Nkhanza zimenezi ziri mmagulu osiyanasiyana monga awa;

### 5.4.3. Mchitidwe Wokakamiza Zogonana

Kukakamiza zogonana ndi mchitidwe omwe umachitika kwa munthu ochepekedwa kuti athandizidwe. Ochita izi amagwiritsa ntchito mphamvu, ndalama, udindo ndi kudziyenereza kosiyanasiyana monga kutchuka pa ndale. Pamene ntchito za Pulogalamu ya RCRP 2 zikukhazikitsidwa komanso kuyendetsedwa, pali kuthekera kuti nkhanzazi zitha kuchitika pakati pa omwe akugwira ntchito komanso kwa anthu okhudzidwa ndi ntchito za Pulogalamuyi ndi maanja awo.

### 5.4.4. Mchitidwe Olimbikitsa Zogonana Mosayenera

Mchitidwewu ndi okakamiza zogonana ponyengelera komanso kugwiritsa ntchito mawu onyonza kapena mphamvu zomwe zingaphwanye ufulu wa munthu. Mchitidweyu umachitika kwambiri malo ogwilira ntchito ndipo nthawi zambiri, okhudzidwa saabwera poyera kunena za nkhanzazi.

### 5.4.5. Kugwilirira

Mchitidwewu umatanthauza kugonana mokakamiza komanso kuopseza. Mchitidwewu ndi waupandu ndipo ndiwophwanya ufulu wa munthu komanso malamulo oyendetsera dziko.

### 5.4.6. Mchitidwe Ogwilirira Ana

Mchitidwewu ndi kugonana ndi msungwana osakwana zaka 18 zakubadwa komanso kwa atsikana omwe ali ndi vuto la mu ubongo ngati misala.

### 5.4.7. Maukwati a Ana Komanso Okakamiza

Uwu ndi ukwati wopanda dongosolo omwe umachitika pakati pa mwana osakwana zaka 18 zakubadwa ndi munthu wamkulu kapena mwana nzake.

### 5.4.8. Mchitidwe wa Nkhanza kwa Amayi ndi Atsikana

Izi ndi nkhanza zomwe zimachitika kwa amayi kapena atsikana zomwe zingachititse kuti avulale pa thupi kapena mmalingaliro. Nkhanza zi zimachitika pogwiritsa ntchito mphamvu komanso kuphwanya maufulu a amayi kapena atsikana. Nkhanzazi zimachitika poopseza, kuumiriza kapena kuphwanya ufulu ndipo ochitiridwa ake ambiri amakhala amayi ndi asungwana mmalo/ mmadera osiyanasiyana.

### 5.4.9. Nkhanza za ku Thupi

Izi ndi nkhanza zokhudza kumenya mu njira zosiyanasiyana monga kufinya kapena kudina pakhosi, kugenda kapena njira ina iliyonse yofuna kuvalazira munthu.

### 5.4.10. Nkhanza zokhudza Chuma

Izi ndi nkhanza zokhudza kukaniza kapena kutsekereza mwayi wopeza chuma, kumuletsa munthu kupanga ziganizo zokomera iye pa katundu kapena ndalama zomwe wapeza kuchokera mu ntchito za Pulogalamu ya RCRP-2 kapena kutenga nawo gawo pa ntchito za banki m'khonde. Nkhanzazi zikuphatikizanso kuononga katundu ndi kulephera kutsatira ndondomeko zoteteza chuma.

### 5.4.11. Nkhanza za M'malingaliro

Nkhanzazi zimachitika pamene okhudzidwa wakakamizika kuchita zinthu zosayenera chifukwa choputidwa kapena kuchitiridwa nkhanza. Nkhanzazi ndi zotsatira za nkhanza zosiyanasiyana monga za pakati pa amayi ndi abambo, nkhanza za pa thupi, mnyozo, zovulazana ngakhale kuopsezedwa ndi munthu amene ali ndi udindo kapena wina aliyense amene sakutengana nawo mbali mu Pulogalamu ya RCRP-2.

### 5.4.12. Kugwiritsa Ntchito Mawu Onyoza

Uku ndi kugwiritsa ntchito mawu otukwana kapena achipongwe omwe cholinga chake ndi kuipitsa mbiri, kunyazitsa kapena kuchitira nkhanza anthu omwe akupindula ndi ntchito za Pulogalamu ya RCRP-2.

## 5.5. MCHITIDWE WA TSANKHO NDI KATANGALE POLEMBA KAPENA KUSANKHA ANTHU OPINDULA NDI PULOGALAMU YA RCRP-2

1 Source: Malawi Communications Regulatory Authority (MACRA) Website (www.macra.mw)

Pamene Pulogamuyi ikuchitika, mphekesera za tsanko, katangale ndi kukondera polemba komanso kusankha opindula ndi pulogalamuyi zitha kutumphuka. Izi zikuyenera kuperekedwa ku makomiti Olandira ndi Kuthetsa Madandaulo kuti achite kalondolondo. Makomitiwa aphunzitsidwa za mmene angakwanitsire kugwira ntchitoyi ndikudziwitsira adindo oyenera monga apolisi.

### 5.6. Kayendetsedwe ka Nkhanza Zobwera Chifukwa cha Kusiyana Pakati Pa Amayi ndi Abambo ndi Zokhudza Mchitidwe Ogonana

Bukuli laika njira zomwe zingatsatidwe popereka malipoti, kafukufuku, kuthetsa kapena kutumiza nkhanza zomwe zingachitike pomwe Pulogalamu ya RCRP-2 ikuchitika.

Nkhanza zobwera chifukwa cha kusiyana pakati pa amayi ndi abambo ndi zosiyana ndi madandaulo ena omwe makomiti Olandira ndi Kuthetsa Madandaulo amalandira. Pachifukwachi, nkhanza za mtunduwu zikuyenera kuyendetsedwa mosunga chinsinsi. Makomiti adziphunzitsidwa za momwe angathandizire okhudzidwa ndi nkhanza zobwera chifukwa cha kusiyana pakati pa amayi ndi abambo komanso zokhudza mchitidwe ogonana monga kagwiritsidwe ntchito ka njira zoperekera malipoti okhudza chisamaliro ndi chitetezo kwa apolisi. A komiti adziperekanso malipoti kwa achipatala kuti okhudzidwa alandire thandizo loyenera monga mankhwala odziteteza ku matenda opatsirana monga HIV ndi AIDS. Malipoti ena adziperekedwanso ku Ofesi yosamalira Anthu kuti okhudzidwa athandizidwe pa nkhani ya mmalingaliro. A komiti adzidziwitsanso mabwalo a milandu kuti okhudzidwa apeze chilungamo. Pulogalamu ya RCRP-2 idzilumikizanso makomiti Olandira ndi Kuthetsa Madandaulo ku makomiti ena olimbikitsa kuthetsa nkhanza. Ena mwa makomiti omwe akupezeka mmadera ambiri ndi monga Othandiza Ovutika ndi Omwe ochitiridwa Nkhanza (CVSUs), Magulu Othana ndi Nkhanza Mmadera (CAGs), komanso atetezi a ana. Makomiti Olandira ndi Kuthetsa Madandaulo a RCRP-2 adzilumikizitsidwa ndi magulu atchulidwawa kuti adzipeza thandizo mosavuta. Kuonjezera apa, makomitiwa adzidziwitsidwa momwe angaperekere malipoti okhudza nkhanza komanso chitetezo cha ana kudzera ku nambala za foni zomwe angaimbe mwaulere ngati izi: 5600 – madandaulo a Nkhanza za pakati pa amayi ndi abambo, 116 – chitetezo cha ana. Mukafuna kupeza zambiri pitani pa tsamba XX (annex 1). Bungwe lomwe lidzithandizira kugwira ntchito zothana ndi nkhanza zochitirana pakati pa amayi ndi abambo lidzilumikizitsidwa ndi Unduna Woona zoti Pasakhale Kusiyana Pakati pa Amayi ndi Abambo, Chitukuko ndi Chisamaliro Cha Anthu.

---

Mchitidwe olimbikitsa zogonana ndi mchitidwe wosayenera komanso ndi umodzi wa nkhanza zomwe zimachitika kwambiri mmalo a ntchito ndipo ambiri saulabadira. Gawo 7 la Lamulo Loona kuti Palibe Kusiyana Pakati pa Amayi ndi Abambo lomwe lidakhazikitsidwa m’chaka cha 2013 likupereka mphamvu ku Boma la Malawi kuti lionetsetse kuti makampani komanso olemba anthu ntchito akhazikitse ndondomeko ndi kuzigwiritsa ntchito pofuna kuthetsa nkhanzazi m’malo antchito. Ngati njira imodzi yothana ndi nkhanza za pakati pa amayi ndi abambo ndi mchitidwe ogonana mosavomerezeka mmalo antchito, RCRP-2 idzilimbikitsa kupanga ndondomeko ndi mfundo zothetsera madandaulo okhudza nkhanza zosiyanasiyana pakati pa ogwira ntchito. (Onani Zowonjezera zachitatu (3) – Chitsanzo cha pulani yake). Bungwe lomwe lidzithandizira kugwira ntchito zothana ndi nkhanza zochitirana pakati pa amayi ndi abambo lidzilumikizitsidwa ndi makhonsolo, ma kontirakita komanso makomiti oona nkhani za madandaulo.Njira Zoyenera Kutsatira Pofuna Kuthana Ndi Madandaulo Okhudza Nkhanza ndi Milandu Yapadera mu Pulogalamu ya RCRP-2

**TABLE 3-4: PROCEDURES TO BE FOLLOWED WHEN HANDLING CASES OF GBV AND OTHER SPECIAL CASES UNDER THE RCRP-2**

| SN | MTUNDU WA MLANDU | MULINGO WA CHIDWI | NDONDOMEKO ZOYENERA KUTSATA | NJIRA YA KATHETSEDWE KA MLANDU |
|---|---|---|---|---|
| 1 | **Nkhanza za Mchitidwe Ogonana** | **Waukulu kwambiri** | • Uwu ndi mlandu waupandu omwe ochitiridwa akuyenera kudziwitsa msanga a Komiti ya Chisamaliro cha Anthu (CBVSU), a polisi (PVSU) kapena Ofesi yachikwanekwane (One Stop Centre).<br>• Ngati membala wa komiti walandira mlanduwu, akuyenera kuti awutumize ku CBVSU, PVSU kapena ofesi yachikwanekwane.<br>• Kwina kotumiza mulandu ngati uwu ndi zipatala zing'onozing'ono, atetezi a ana m'dera, komanso alangizi achitukuko m'dera.<br>• Odandaula atha kutumizanso madandaulo kudzera ku nambala za foni zomwe zimaimbidwa mwaulere monga 116. Poonjezera apa, Pulogalamu ya RCRP-2 ikhala ndi nambala za foni zomwe okhudzidwa adziimba mwaulere.<br>• Onetsetsani kuti ochitiridwa nkhanza watumizidwa ku chipatala pasanathe maola 72 chichitikireni nkhanzayo.<br>• Lembani mu Fomu yokhudza milandu/madandaulo ndikutumiza ku Banki Yaikulu (World Bank) kudzera ku Ofesi ya RCRP-2 PCU pasanathe maola 48 kuchokera pomwe mlandu wadziwika. | • Ochitiridwa nkhanza akuyenera kuthandizidwa mwaulemu ndi moyenera.<br>• Ochitiridwa nkhanza akuyenera kupatsidwa uthenga wa momwe angaperekere dandaulo .<br>• Ndi chilolezo chochokera kwa ochitiridwa nkhanza, membala wa komiti atha kuperekeza odandaulayo koyenelera.<br>• Ochitiridwa nkhanza akuyenera kusungiridwa chinsinsi komanso dzina lake lisalembedwe pa fomu Yolandilira ndi Kuthetsera Madandaulo. Ngakhale izi ziri chonchi, ngati ochitiridwa nkhanza wapereka chilolezo, omenyera ufulu wa anthu akuyenera kulemba momwe nkhani yachitikira.<br>• Ngati opalamulayo ali munthu yemwe akugwira nawo ntchito za Pulogalamu ya RCRP2; ndipo kuti lamulo silidagwirepo ntchito pa iye, komiti Yolandira ndi Kuthetsa Madandaulo idzitumiza nkhaniyo ku komiti ya pa boma kuti iyendetsedwe moyenera. |

| SN | MTUNDU WA MLANDU | MULINGO WA CHIDWI | NDONDOMEKO ZOYENERA KUTSATA | NJIRA YA KATHETSEDWE KA MLANDU |
|---|---|---|---|---|
| 2 | **Nkhanza za pa Thupi** | **Waukulu kwambiri** | • Ochitiridwa nkhanza atha kukadandaula mwachindunji ku CBVSU kapena PVSU.<br>• Ochitiridwa nkhanza atha kukadandaula ku komiti Yolandira ndi Kuthetsa Madandaulo.<br>• Ochitiridwa nkhanza athandizidwe mwamsanga ndi moyenera ndipo zotsatira zomwe zipezekezo zitumizidwe ku VSU kapena ku chipatala.<br>• Komiti ikuyenera kuyambitsa kafukufuku wa dandaulo.<br>• Ngati mlanduwu ukukhudza munthu wa udindo; dandaulo/mlanduwo ukuyenera kutumizidwa ku komiti yaikulu. | • Ochitiridwa nkhanza akuyenera kuthandizidwa mwaulemu ndi moyenera.<br>• Lembani tsatanetsatane wa dandaulo kuphatikizapo mbiri ya wochita nkhanza.<br>• Kafukufuku wa nkhani ayambike.<br>• Komiti ikuyenera kudziwitsa odandaula zotsatira ikamaliza kuchita kafukufu wake.<br>• Odandaula akuyenera kuuzidwa zonse zoyenelera ngati dandaulo lake likufunika kutumizidwa ku makomiti potengera kuti dandaulolo ndi lokhudza milandu ya upandu.<br>• Ngati ochita nkhanza ndi otsogolera ntchito kapena membala wa komiti, mtsogoleriyo/ membalayo akuyenera kuchotsedwa mu ntchito za Pulogalamu ya RCRP-2. |
| 3 | **Nkhanza pa Chuma** | **Wapakatikati** | • Ochitiridwa nkhanza atha kupereka dandaulo lake ku komiti.<br>• Komiti idzichita kafukufuku wa dandaulo pofuna kudziwa ngati wochita nkhanza ali munthu wa m'deralo kapena ogwira nawo ntchito ya Pulogalamu ya RCRP-2.<br>• Ngati dandaulo kapena mlandu ndi wokhudza nkhani za m'banja, komiti idzitumiza nkhaniyi ku Ofesi Yoona za Chisamaliro cha Anthu kapena ku mabungwe komanso magulu omwe si a boma. | • Lembani tsatanetsatane wa dandaulo komanso mbiri ya wochita nkhanza.<br>• Kafukufuku wa mulandu ayambike<br>• Komiti ikuyenera kugwirizana za chigamulo ndi mmene odandaula adziwitsidwire.<br>• Ngati ochita nkhanza ndi otsogolera ntchito kapena membala wa komiti, mtsogoleriyo/ membalayo akuyenera kuchotsedwa mu ntchito za Pulogalamu ya RCRP-2. |

| SN | MTUNDU WA MLANDU | MULINGO WA CHIDWI | NDONDOMEKO ZOYENERA KUTSATA | NJIRA YA KATHETSEDWE KA MLANDU |
|---|---|---|---|---|
| 4 | **Nkhanza za M'malingaliro** | **Wapakatikati** | • Ochitiridwa nkhanza atha kupereka dandaulo ku komiti.<br>• Komiti idzichita kafukufuku wa dandaulo pofuna kudziwa ngati wochita nkhanza ali munthu wa m'deralo kapena wogwira nawo ntchito ya Pulogalamu ya RCRP-2.<br>• Ngati dandaulo kapena mlandu ukukhudza nkhani za m'banja, komiti idzitumiza nkhaniyi ku Ofesi Yoona za Chisamaliro cha Anthu kapena ku mabungwe ndi magulu omwe si a boma. | • Lembani tsatanetsatane wa dandaulo komanso mbiri ya wochita nkhanza.<br>• Kafukufuku wa mlandu ayambike<br>• Komiti ikuyenera kugwirizana za chigamulo ndi mmene idziwitsire odandaula za chigamulocho.<br>• Ochitiridwa nkhanza akuyenera kuuzidwa zonse zoyenelera ngati dandaulo kapena mlandu ukufunika kutumizidwa ku komiti ina kapena ngati uli waupandu.<br>• Ngati ochita nkhanza ndi otsogolera ntchito kapena membala wa komiti, mtsogoleriyo/membalayo akuyenera kuchotsedwa mu ntchito za Pulogalamu ya RCRP-2. |
| 5 | **Nkhanza kwa Amayi ndi Atsikana** | **Waukulu kwambiri** | • Mlandu okhudza upandu udzatsegulidwa ndipo ochitiridwa nkhanza atha kupereka dandaulo lake mwachindunji ku CBVSU, PVSU kapena ofesi yachikwanekwane.<br>• Ngati dandaulo lalandiridwa ndi membala wa komiti, membalayo akuyenera kutumiza dandaulolo ku CBVSU, PVSU kapena ofesi yachikwanekwane.<br>• Malo ena omwe odandaulayo angapite ndi ku chipatala, kwa alangizi a za chitetezo cha ana kapena achitukuko. | • Ochitiridwa nkhanza akuyenera kuthandizidwa mwaulemu ndi moyenera.<br>• Ochitiridwa nkhanza akuyenera kuuzidwa zonse zoyenelera ngati dandaulo kapena mlandu ukufunika kutumizidwa ku komiti ina, kapena dandaulo liri lokhudza upandu.<br>• Ndi chilolezo chochokera kwa ochitiridwa nkhanza, membala wa komiti atha kuperekeza odandaulayo koyenelera.<br>• Ochitiridwa nkhanza akuyenera kusungiridwa chinsinsi komanso dzina lake lisalembedwe mu fomu Yolandilira ndi Kuthetsera Madandaulo. Ngakhale izi ziri chonchi, ngati ochitiridwa nkhanza wapereka chilolezo, omenyera ufulu wa anthu akuyenera kulemba za momwe nkhani yachitikira.<br>• Ngati opalamulayo ndi wogwira nawo ntchito za Pulogalamu ya RCRP2 ndipo kuti lamulo silidagwirepo ntchito pa iye, komiti Yolandira ndi Kuthetsa Madandanulo idzitumiza nkhaniyo ku komiti ya pa boma kuti iyendetsedwe moyenera |

| SN | MTUNDU WA MLANDU | MULINGO WA CHIDWI | NDONDOMEKO ZOYENERA KUTSATA | NJIRA YA KATHETSEDWE KA MLANDU |
|---|---|---|---|---|
| 6 | **Kugwiritsa Ana Ntchito Zoposa Msinkhu Wawo** | **Waukulu** | • Ochitiridwa nkhanza kapena membala kapena aliyense yemwe waona izi, adziwitse komiti mwamsanga.<br>• Ochitiridwa nkhanza apatsidwe thandizo loyambirira kenako atumizidwe ku chipatala.<br>• Fomu yokhudza mlandu/dandaulo iyenera kulembedwa ndipo itumizidwe ku Banki Yaikulu kudzera ku Ofesi ya RCRP2 PCU pasanathe maola 48 kuchokera pomwe mlandu wadziwika. | • Lembani tsatanetsatane wa dandaulo komanso mbiri ya wochita nkhanza.<br>• Kafukufuku wa mlandu ayambike<br>• Komiti ikuyenera kugwirizana za chigamulo ndi mmene idziwitsire odandaula za chigamulocho.<br>• Ochitiridwa nkhanza akuyenera kuuzidwa zonse zoyenelera ngati dandaulo kapena mlandu ukufunika kutumizidwa ku komiti ina kapena ngati uli waupandu.<br>• Ngati wochita nkhanza ndi otsogolera ntchito kapena membala wa komiti, mtsogoleriyo/membalayo achotsedwe mu ntchito za Pulogalamu ya RCRP-2. |
| 7 | **Kuzembetsa ana** | **Waukulu** | • Ochitidwa nkhanza kapena membala yemwe waona izi, adziwitse komiti mwamsanga.<br>• Ochitidwa nkhanza apatsidwe thandizo loyambirira kenako atumizidwe ku chipatala.<br>• Fomu yokhudza mlandu/dandaulo ilembedwe ndipo itumizidwe ku Banki Yaikulu kudzera ku Ofesi ya RCRP 2 PCU pasanathe maola 48 kuchokera pomwe mlandu wadziwika. | • Lembani tsatanetsatane wa dandaulo komanso mbiri ya wochita nkhanza.<br>• Kafukufuku wa mlandu ayambike<br>• Komiti ikuyenera kugwirizana za chigamulo ndi mmene idziwitsire odandaula za chigamulocho.<br>• Ochitiridwa nkhanza akuyenera kuuzidwa zonse zoyenelera ngati dandaulo kapena mlandu ukufunika kutumizidwa ku komiti ina kapena ngati uli waupandu.<br>• Ngati wochita nkhanza ndi otsogolera ntchito kapena membala wa komiti, mtsogoleriyo/membalayo achotsedwe mu ntchito za Pulogalamu ya RCRP-2. |

| SN | MTUNDU WA MLANDU | MULINGO WA CHIDWI | NDONDOMEKO ZOYENERA KUTSATA | NJIRA YA KATHETSEDWE KA MLANDU |
|---|---|---|---|---|
| **8** | **Kuvulala kapena kuchita ngozi zodzetsa imfa** | **Waukulu** | • Ochitiridwa nkhanza kapena membala yemwe waona izi, adziwitse komiti mwamsanga.<br>• Ochitiridwa nkhanza apatsidwe thandizo loyambirira kenako atumizidwe ku chipatala.<br>• Fomu yokhudza mlandu/dandaulo iyenera kulembedwa ndipo itumizidwe ku Banki Yaikulu kudzera ku Ofesi ya RCRP 2 PCU pasanathe maola 48 kuchokera pomwe mlandu wadziwika. | • Tsatanetsatane wa dandaulo kuphatikizipo mbiri ya wochita nkhanza zilembedwe.<br>• Kafukufuku wa mlandu ayambike<br>• Komiti ikuyenera kugwirizana za chigamulo ndi mmene idziwitsire odandaula za chigamulocho.<br>• Ochitiridwa nkhanza akuyenera kuuzidwa zonse zoyenelera ngati dandaulo kapena mlandu ukufunika kutumizidwa ku komiti ina kapena ngati uli waupandu.<br>• Odandula akuyenera kupatsidwa ndondomeko zokwanira ngati dandaulo lake silingathetsedwe ndi komiti Yolandira ndi Kuthetsa madandaulo komanso ngati dandaulo liri lokhudza ndi mlandu wa upandu.<br>• Ngati wochita nkhanza ndi otsogolera ntchito kapena membala wa komiti, mtsogoleriyo/membalayo achotsedwe mu ntchito za Pulogalamu ya RCRP-2. |

# MNDANDANDA WA ZOONJEZERA

## ZOONJEZERA ZOYAMBA (ANNEX 1): NDONDOMEKO ZOYENERA KUTSATA POTHANDIZIRA YEMWE WAKHUDZIDWA NDI NKHANZA ZOOPSA MONGA KUGWIRIRIDWA KOMANSO MILANDU YOKHUDZA MATENDA OPATSIRANA POGONANA MOSADZITETEZA MONGA HIV NDI AIDS

<table>
<tr><td rowspan="2">1</td><td colspan="2">PAMENE DANDAULO KAPENA NKHANZA YATSIMIKIZIKA: OCHITIRIDWA NKHANZA KAPENA AMENE WAONA NKHANZA AYENERA KUUZA MUNTHU YEMWE AMAMUKHULUPIRIRA, KOMITI YOLANDIRA NDI KUTHETSA MADANDAULO KAPENA OGWIRA NTCHITO ZOTHANA NDI NKHANZA.</td></tr>
<tr><td colspan="2">NDONDOMEKO<br>• Khalani oleza mtima, omvetsera mwachidwi, osathamangira kuweruza, owonetsa kukhudzidwa, komanso okhulupilira zomwe ochitiridwa nkhanza akudandaula.<br>• OSALOZA CHALA OCHITIRIDWA NKHANZAYO KUTI NDI WOLAKWA, mutsimikizireni kuti athandizidwa moyenera.<br>• Pomwe mukumuthandiza ochitiridwa nkhanza, tsatirani ndondomeko monga KUSUNGA CHINSINSI, CHITETEZO, NDI ULEMU nthawi zonse.<br>• Chezani ndi odandaula pa malo otetezeka, ndipo onetsatsani kuti odandaulayo akuthandizidwa ndi munthu ofanana naye chibadwidwe . MUSACHEZE ndi odandaula pa gulu kapena pa malo omwe anthu ena atha kumvera zokambiranazo.<br>• FUNSANI mafunso ofunikira okha, musamuchititse odandaula kuyankhula nkhani yake mobwerezabwereza. Musamukakamize odandaula kuyankhula zinthu zomwe saakufuna. OSAMUFUNSA odandaula kuti ndi chifukwa chani zidamuchitikira. MUSACHITE KAFUKUFUKU NGATI NDI INU APOLISI. Udindo wanu ndi wopereka chilimbikitso ndi thandizo.<br>• Nthawi zones, onetsetsani kuti CHISAMALIRO NDI CHITETEZO cha odandaula ziri patsogolo pa ntchito yanu, komanso perekani chitetezo kwa ogwira ntchito, mboni, odzipereka ndi ena.<br>• Zindikirani kuti odandaula akapereka dandaulo, chiopsezo pa moyo wake chimatha kukula ndipo onetsetsani kuti mwachita zoyenera kuti asakhale pa chiopsezo kapena kuti nkhanza isachitikenso kwa iye.<br>• Muthandizireni odandaulayo kupeza munthu yemwe angamukhulupilire mdera lomwe iye amakhala monga mzake wapamtima, mbale kapena munthu wina kuti adzitha kumumasukira ngati pangafunike kutero. Perekani zambiri zokhudza ntchito zothandiza wokhudzidwa. Perekani uthenga okwanira komanso odalirika okhudza thandizo lomwe ochitiridwa nkhanza angathe kulipeza.</td></tr>
<tr><td>2</td><td>Kwa ana (munthu aliyense yemwe sanakwanitse zaka 18 zakubadwa)<br>• ZOFUNA ZA MWANA zidzikhala patsogolo nthawi zonse.<br>• Kutenga nawo gawo popanga ziganizo kudalire msinkhu kapena kukhwima nzeru kwake.<br>• Malinga ndi Gawo 36 la lamulo Lachisamaliro cha Ana, Chitetezo komanso Chilungamo, milandu yonse yokhudza nkhanza kwa ana idzitumizidwa kwa adindo oyenera.</td><td>Kwa akulu (kwa aliyense oposa zaka 18 zakubadwa )<br>Musapange chiganizo popanda kupeza chilolezo kuchokera kwa munthu ochitiridwa nkhanza.<br>Uthenga ulionse usagawidwe popanda chilolezo cha odandaula.<br>Mulolereni odandula kupanga chiganizo chake ndi kulandira thandizo loyenera. Pachifukwachi, muthandizeni ndi upangiri kuti odandaulayo apange chiganizo choyenera.</td></tr>
</table>

## 3

| | |
|---|---|
| **Perekani thandizo la msanga kwa ana!**<br>**Chitetezo chikhale patsogolo!**<br><br>**NGATI PALI CHIOPSEZO CHOMWE CHINGABWERETSE IMFA:**<br>Dziwitsani adindo oyenera monga apolisi, a Chitetezo Cha Mmudzi kapena thandizo lina monga nyumba yotetezeka yosungiramo anthu Ochitiridwa Nkhanza yomwe ili m'deramo kapena kwina NGATI njira imeneyi siingayike odandaula pa chiopsezo chirichonse. Kuphatikiza apo, thandizo la kuchipatala likhale patsogolo. | **Kwa Akulu – Pamene odandaula wapereka chilolezo**<br><br>**Perekani thandizo la kuchipatala msanga!** |

## 4

**NKHANZA ZOGONANA**

Onetsetsani kuti munthu walandira thandizo lachipatala msanga (monga PEP, EC) pasanadutse masiku atatu (maola 72) pofuna kuchepetsa chiopsezo chotenga kachilombo ka HIV komwe kamayambitsa AIDS. Ngakhale izi ziri chonchi, dandaulo la nkhanzali likuyenera kutumizidwa kwa adindo ena kuti agwirepo ntchito.

**NKHANZA ZA KUTHUPI**

Pitani kuchipatala kuti odandaula akalandire thandizo ngati akumva kupweteka, akutuluka magazi kapena akufunikira thandizo lina losakhudza mabala okhudza ndi kugonedwa.


## 5

**POMWE ZOSOWA ZAMSANGAMSANGA ZATHEKA. POMWE OCHITIRIDWA NKHANZA SAKUFUNIKIRA ZOSOWA ZINA MSANGA MONGA CHITETEZO KAPENA THANDIZO LA CHIPATALA, FUFUZANI ZOSOWA ZAKE ZINA NDIPO MUTUMIZENI KWINA KOMWE ZILIPO.**

**THANDIZO LACHIKWANEKWANE KWA OCHITIRIDWA NKHANZA:** Izizikutanthauza kuti adindo awonetsetse kuti ochitiridwa nkhanza wapeza thandizo loyenera, lopezeka mosavuta komanso lapamwamba lomwe ndi kuphatikizapo chisamaliro chamoyo, mmalingaliro, chitetezo komanso kupeza chilungamo ku mabwalo a milandu.

| THANDIZO LA CHIPATALA | KAYENDETSEDWE KA MILANDU/ NKHANI KOMANSO CHITHANDIZO CHA M'MALINGALIRO | CHISAMALIRO NDI CHITETEZO | THANDIZO LA MALAMULO NDI KUPEZA CHILUNGAMO |
|---|---|---|---|
| • Chipatala cha pa boma.<br>• Ofesi yachikwanekwane, chipatala cha kudera.<br>• Chipatala chaching'ono.<br>• Alangizi a zaumoyo a m'dera. | • Ofesi yoona chisamaliro cha anthu pa boma (DSWO).<br>• Mtetezi wa Ana mdera (CPW).<br>• Nthambi ya polisi yothana ndi nkhanza (PVSU).<br>• Nthambi ya Kudera Yothana ndi Nkhanza (CVSU)<br>• Nambala ya foni yoimba mwaulere; yoperekera dandaulo la nkhanza kwa ana m'dziko lonse - 116<br>• Nambala ya foni yoimba mwaulere yoperekera madandaulo a nkhanza – 5600.<br>• Nambala ya foni yoimba mwaulere yoperekera madandaulo pansi pa Pulogalamu ya RCRP-2.<br>• Mabungwe omwe si-aboma, a m'dera komanso achipembedzo. (NGO/CBO/FBO). | • Polisi ya pa boma.<br>• Polisi yaying'ono.<br>• Magulu a mmadera.<br>• Nthambi ya polisi yothana ndi nkhanza (VSU).<br>• Nthambi ya polisi ya m'dera yothana ndi nkhanza (CVSU). | • Khoti la Magistrate.<br>• Khoti la ana.<br>• Alezi a malamulo (paralegals).<br>• Mabungwe omwe si aboma, a m'dera komanso achipembedzo (NGO/ CBO/FBO). |

# ZOWONJEZERA ZACHIWIRI: NJIRA ZOTUMIZIRA MADANDAULO KAPENA MILANDU ZOKHUDZA NKHANZA ZOGWILIRIRA KAPENA KUGONANA MOKAKAMIZA (GBV/SEA/SH)



## ZOONJENZERA ZACHITATU: CHITSANZO CHA KALEMBEDWE KA PULANI YOTHANA NDI NKHANZA ZA PAKATI PA AMAYI NDI ABAMBO (GBV)

| ZOOPSA NDI ZOYENERA KUGANIZIRAPO | KAPEWEDWE KA NKHANZA KOMANSO MMENE ANTHU ANGATHANDIZIKIRE AKACHITIRIDWA NKHANZA | AKALOZERA (INDICATORS) | ADINDO OYENERA KUGWIRA NTCHITOYO | NTHAWI YOGWILIRA NTCHITOYO |
|---|---|---|---|---|
| Mwachitsanzo: Nthawi zambiri amayi ndi asungwana amasalidwa ndiponso amakhala pa chiopsezo chachikulu chochitiridwa nkhanza monga kugwiliridwa kapena kugonedwa mokakamizika (SEA/SH) m'malo omwe mukugwirika ntchito za zomangamanga. | Mwachitsanzo: Kupereka maphunziro komanso kudziwitsa anthu za nkhanza zomwe amayi amakumana nazo. Opindula ndi Pulogalamu ya RCRP-2 adziwitsidwe za malamulo, komwe angatule nkhawa zawo komanso thandizo lomwe anagapeze akachitiridwa nkhanza. | Chiwerengero cha misonkhano yodziwitsa anthu m'madera. | Kuchita ntchito: Komiti ya PCU, othandizira pa ntchito zothana ndi nkhanza komanso makontarakitala. | Nthawi yomwe ntchito za Pulogalamu ya RCRP-2 zisadayambe. |
| **ZOOPSA NDI ZOYENERA KUGANIZIRAPO** | **KAPEWEDWE KA NKHANZA KOMANSO MMENE ANTHU ANGATHANDIZIKIRE AKACHITIRIDWA NKHANZA** | **AKALOZERA (INDICATORS)** | **ADINDO OYENERA KUGWIRA NTCHITOYO** | **NTHAWI YOGWILIRA NTCHITOYO** |
| Mwachitsanzo: Amayi ndi asungwana amakakamizika kuchita zibwenzi zogonana ndi amisiri oyang'anira ntchito za zomangamanga ngati malipiro kuti alembedwe ntchito kapena akonderedwe mu njira zina. | Mwachitsanzo: Amayi ndi asungwana omwe achitiridwa nkhanza atumizidwe komwe akalandire thandizo. | Chiwerengero cha amayi ndi asungwana omwe akulandira thandizo. | Makomiti a PCU, PIU, othandizira pa ntchito zothana ndi nkhanza. | Nthawi imene ntchito za Pulogalamu ya RCRP-2 zikuchitika. |

## ZOONJEZERA ZA CHINAYI (4): FOMU YOLEMBAPO MADANDAULO OCHOKERA KU MAKOMITI A MMAKHONSOLO, M'DERA/MU WODI /A OGWIRA NTCHITO (CGRMC/ WARD GRMC/WORKERS) KOMANSO FOMU YA MATHETSEDWE A MADANDAULO

## FOMU YOLEMBAPO MADANDAWULO OCHOKERA KU MAKOMITI AMADANDO

### GAWO LOYAMBA: ZOKHUDZA ODANDAULA

| | | | | |
|---|---|---|---|---|
| Boma: | Mfumu yandodo: | | | Dzina la Gulupu: |
| Name of the Sub-Project: | Location (Village): | | | Tsiku lopereka dandaulo: |
| **Dzina la odandaula:** | Dzina la pulojekiti pansi pa RCRP 2 | Gawo la ntchito | Nambala ya lamya | Email Address: |
| **Chomwe munthu ali:** Mamuna ◯ Mkazi ◯ | RCRP-2 ◯ | | | |

### GAWO LACHIWIRI: TSATANETSATANE WA DANDAULO

| Nambala ya chochitika # | Tsiku lodandaulira | Kodi ndandaulo ndi lotumizidwa kapena latsopano | | Tsiku lofufuzira | Dzina la munthu ofufuza |
|---|---|---|---|---|---|
| | | latsopano ◯ | Lotumizidwa ◯ | | |

| Kufotokoza dandaulo | Kathetsedwe ka nkhani |
|---|---|
| | |

| Mtundu wa dandaulo: | Lokhudaza ntchito ◯ | Lokhudza malo ◯ | Lokhudza Nkhaza (GBV/SEA) ◯ | Lokhudza Katangale ◯ | Zina ◯ | Ngati ndi zina fotokozerani |
|---|---|---|---|---|---|---|
| Name of the Person recording the issue: | | | | | | |

| GAWO LACHITATU: KUTSEKA DANDAULO | | | GAWO LACHINYI: KUTUMIZA DANDAULO KWINA | |
|---|---|---|---|---|
| Ngati dandaulo lathetsedwa, sayinani apa: | | | Latumizidwa ku: | Nambala ya dandaulo: |
| | | | Tsiku: | Munthu yemwe akutsatira nkhaniyi: |
| | Dzina | kusayina | | |
| Wapampando wa komiti ya GRM: | | | Chiganizo chothetsa nkhani: | |
| Odandaula: | | | | |
| Mlembi wa komiti ya GRM: | | | | |

### GAWO LA CHISANU: CHITSIMIKIZO CHAKULANDIRA DANDAULO

| | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|
| Dandaulo: | | | Nambala ya fomu: | | |
| Mfumu ya ndodo | | Mmene ndandaulo liliri: | | Latsopano | Latumizidwa kuchokera kwina |
| Dzina la odandaula | | Olandira lipoti: | | Nambala ya foni yochitilapo kalondolondo: | |

# ZOONJEZERA FOMU YOLOWETSERA MADANDAULO

KAUNDULA WA MADANDAULO MU PULOGALAMU YA RCRP-2

| SN | TSIKU LOYAMBA KUMVA DANDAU-LO | ODANDAULA | ODANDA-ULIDWA | MFUMU YANDO-DO | BOMA | MTUNDU WA DANDAULO | NKHANI | CHIGANIZO PA DANDAULO | | | MAU OWON-JEZERA | TSIKU LOTSE-KEDWA |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | | | | Sichi-naper-eked-we | Chaper-ekedwa ndipo dandau-lo latse-kedwa | Dandauulo latumizid-wa kwina | | |
| | | | | | | | | | | | | |
| 1 | | | | | | | | | | | | |
| 2 | | | | | | | | | | | | |
| 3 | | | | | | | | | | | | |
| 4 | | | | | | | | | | | | |
| 5 | | | | | | | | | | | | |
| 6 | | | | | | | | | | | | |
| 7 | | | | | | | | | | | | |
| 8 | | | | | | | | | | | | |
| 9 | | | | | | | | | | | | |
| 10 | | | | | | | | | | | | |
| 11 | | | | | | | | | | | | |
| 12 | | | | | | | | | | | | |